### C. LILONGWE : LIKULU LA DZIKO LA MALAWI

Kusamutsa kwa Likulu la Boma la Malawi pa 1 Januwale, 1975, kuchokera ku Zomba m'Chigawo Chakumwera kupita ku Lilongwe m'Chigawo Chapakati, kwawonetsa poyera chitukuko cha dziko lino, chimene chachitika chifukwa cha maganizo a mphamvu ndi anzeru a mtsogoleri wake, Wolomekezeka Prezidenti Wanuyaya, Ngwazi Dr. H. Kamuzu Banda.

Ntchito yomanga Likulu latsopanolo idayambika m'chaka cha 1969 momwemu. Kuyambira panthawiyo, anthu a bizinesi ndi anthu ena wamba agwiritsa ntchito ndalama zopyola pachiweregero cha K50-million, zimene zathandiza kutukula madera a nthaka yachonde ku Zigawo izi: Zapakati ndi Kumpoto.

Kutukula kwa Mzinda wa Lilongwe, idaali imodzi mwa ntchito zofunika kwambiri m'maganizo ake a Prezidenti Wanuyaya, pofuna kutukula miyoyo ya anthu ake, pamene iyeyo adaali m'ndende ya ku Gwelo panthawi yomenyera ufulu wa dziko lino.

Pamene Likulu la dziko lino lidaali ku Zomba, ntchito za chitukuko zimene zindachitika m'Chigawo Chakumwera kokha. Chifukwa cha ichi, anthu adaali kusamuka kuchokera kumadera a Kumpoto ndi a Pakati padziko lino, kumka ku Chigawo Chakumwera, kotero kuti chiweregero cha anthu a m'Chigawochi chidaakwera kwambiri; chiweregero cha anthu a Kumpoto chinkalowa kawiri ndi theka poyerekeza ndi cha a m'Chigawo Chakumwera.

Kunkasowanso maofesi atsopano a Boma. Maofesi amene adaalipo panthawiyo ku Zomba adaali aang'ono kwambiri, kotero kuti kudaali koyenera kusamutsa maofesi a madipatimenti ena a Boma kupita ku Blantyre, umene uli ulendo wautali wokwana mitunda makumi anayi. Kusamukako kudaagawa mphamvu ya kayendetsedwe ka ntchito za Boma, ndipo kuyendayenda kwa pakati pamalo awiriwa kudaali kotopetsa ndi kolowa m'thumba.

## LILONGWE : CAPITAL OF MALAWI

The move of the Capital of Malawi on January 1, 1975, from Zomba in the south to Lilongwe in the Central Region highlights the achievements of a nation stimulated to planned, practical progress by its inspired leader, His Excellency the Life President, Ngwazi Dr. H. Kamuzu Banda.

Construction work on the new Capital began only in 1969. Since then, investment by the public and private sector has topped K50-million, bringing a new era of development to the fertile Central and Northern Regions.

The development of Lilongwe was one of the most important aspects of the Life President's program for improving the standard of living of his people, conceived while he was in Gwelo Prison during the struggle for freedom.

With the Capital in Zomba, development that had taken place during the colonial days had been concentrated in the south. This in turn had meant a migration of people away from the north and center of the country, resulting in population densities two-and-a-half times higher in the south than in the north.

There was also a need for new Government office accommodation. Existing offices in Zomba had become too small, and several departments had been forced to move to Blantyre, 40 miles away, splitting the administration and causing communications difficulties.

Likulu latsopanoli lathetsa mavuto awiriwa ndi kuwapatsa anthu ambiri mwawi wopeza ntchito kumalowo, ndipo ntchito za ulimi ndi za malonda zapita mtsogolo kosaneneka.

Likulu latsopanoli, ndi lomwe lathandizira pachitukuko cha dziko lina la Malawi, ndi chitsimikizo chenicheni choonetsa zipatso za ufulu wa Boma loyima palokha.

428

The new Capital is solving both these problems, while at the same time creating new employment opportunities, and both agriculture and commerce have gone ahead greatly.

The new Capital and its contribution to the development of Malawi is indeed a concrete example of the fruits of Independence.

## D. MOYO PA PULAZI

Nditamaliza maphunziro anga a kasamalidwe ka ziweto ndi za ulimi kwa Chitedze, ndinakalowa ntchito papulazi ku Mchenga. Nthawi imeneyo nkuti ndisanakwatire.

Anandipatsa nyumba ya denga (tsindwi) labwino lamalata, losadontha; mazenera abwino achitsulo kutchinjiriza mbala. Pansi anandiikira simenti koti sitimazira ndi dothi kaya ndowe. Inali yokulungiza ndi njereza: inali nyumba yamakono. Ny jophikira inali padera, ndipo anaikamo chitofu osati mafuwa, koti nkhuu zimayaka bwino ndithu; chopika chilichonse chinali kupsa mwamsanga.

Ndinali kusunga ziweto zosiyanasiyana monga izi: ng'ombe, zalinunda ndi zopanda linunda, nkhusa (abira, mberere), mbuzi, nkhumba, abulu, mahatchi ndi agalu ondithandiza kuthamangitsa zilombo zikabwera kuti zithyole makola pofuna kuti zidye ziwetozo. Zilombo zimene zimakonda kuvuta kawirika-wiri ndi afisi, akambuku (anyalubwe). Nthawi zina mikango imavutitsanso ili kubangula.

Zoweta zina za mtundu wa mbalame zimene ndimasamala ndi nkuku, nkuku ndembo, abakha ndi nkunda. Mtundu wa nkuku zimene ndimakonda kusunga ndi mtundu wa meteke chifukwa sizimafa ndi chideru (chitopa) kawirika-wiri. Nkuku za mazira ndi atambala a zitsukwa zazitali, lipombo lalikulu ndi zilimba zakuthwa zazitali ndinali nazonso. Abakha ndiye sindimawakonda kwenikweni chifukwa cha uve wowononga pakhomo ndi chitosi chamadzimadzi.

## LIFE ON AN ESTATE

By J.J. Chiwala Banda

At the end of my study in animal husbandry and agriculture at Chitedze, I was employed at an estate at Mchenga. That was before I married.

I was accommodated in a good iron-roofed house, which never leaked; its good metal windows had burglar's bars. The floor was cemented so that we never smeared it with soil or cattle dung. It was whitewashed; it was a modern house. The kitchen was apart from the main building and in it was a stove, not fireplace stones, so that the firewood burned very well; everything we cooked was ready within a short time.

I was keeping different kinds of livestock such as cattle (humped and unhumped), sheep, goats, pigs, donkeys, horses and dogs to help me chase wild animals if they came and broke the corral in an attempt to eat the domestic animals. The wild animals which gave us trouble frequently were hyenas and leopards. Sometimes lions, which roared, also gave us trouble.

Some domestic animals of the bird class which I was caring for were hens, turkeys, ducks and doves. The type of hens which I liked to keep was that with no feathers on the neck because they resisted Newcastle disease very often. Hens for laying eggs and cocks with

Ng'ombe zimene ndimasunga zinali zonenepa bwino ndipo zinali mitundu iwiri: za mkaka ndi za nyama. Timatole tikabadwa, ndimatiotcha ndi chitsulo cha moto pamene pamati padzamere nyanga. Chonco sizimamera nyanga. Cholinga chinali chakuti podzagulitsa zidzalemere malibisi ambiri pasikelo. Izi ndimachita ndi timatole tamphongo ndi tatikazi tomwe. Koma timatole tatimuna ndimatithena kuti tikadzakula, tidzalemere malibisi ambiri pasikelo ndi kutinso zidzakhale ndi mphamvu (nkhongono) zambiri zokokera ngolo. Zoterezi timati mitheno, zopanda nyanga timati chipundi (njuma) ndipo ng'ombe zazikazi zosabereka timati nzidzi.

Ndinali ndi antchito makumi asanu ndi anayi ondithandiza. Okama mkaka, odyetsa ziweto za mtundu wa mba'ame, nkhumba, otolera mazira, olima kuminda kubzala ndi kukolola.

Kumene kumagona antchitowa ndi mbali ya fama yomweyo kumene kunamangidwa nyumba zawo. Nyumbazi zinali za ndendera zomangidwa ndi zipangizo izi: nsichi, nsungwi, luzi, khonje nsanamila, mzati, phaso, chitseko cha tsekera ndi masindwi ake anali ofoleredwa ndi udzu. Zinalinso zomata ndi zozungulizidwa ndi mipanda. Osalephera nyumba ili yonse inali ndi kanyumba ka chimbudzi potero. Chiwawa kaya kumenyana sizimachitika kawirikawiri chifukwa ndinasankha munthu wamkulu ndi wofatsa kuti aziwayang'anira antchitowo.

Dzinja likabwera, ulimi umagundikanso. Timalima chimanga, khobwe, nyemba, mtedza (nsawa), nzama, nsenjere, udzu ndi mbatata za kachewere. Chimanga kwenikweni chinali cha ng'ombe ndi ziweto zina. Ndimapanga chakudya cha nthawi ya ng'amba ndi chimangacho chisanakhwime, chitangoyamba ngalale (ngalangala) ndevu ndipo ana ali anthete. Ndimakumba nkhuti ndikudula chimangacho ndi kuchikwirira (fotsera) m'nkhuti muja. Nthawi ya



long tail feathers, a big crest and sharp long, long nails on their feet were also kept. I never liked ducks mostly because of their habits of spoiling around the house with their watery droppings.

The cattle which I kept were fat and were of different types; for milk, and for beef. When calves were born I was branding them with a hot metal on the spot where the horn would have grown. For this reason they never grew horns. The reason for doing this was that when selling they should be heavy. I was doing this both to the male and female calves. But the male calves were castrated so that when they grew they should be very heavy and that they should be strong enough to pull the wagon. Such castrated male calves were called oxen, those without horns were called hornless and the female cattle which wouldn't give birth to young ones were called unproductive.

I had ninety employees under me. Some were milking the cows, some were feeding the birds, pigs, picking up eggs, digging the garden, planting and harvesting.

The place where these employees (laborers) were accommodated was on the other side of the farm where ~~their~~ houses were built. These houses were round and were built using poles, bamboo, bark fibers, sisal, verandah poles, central poles, beams, doors made of big grass stalks, and grass thatched roofs. They were also mud packed and surrounded by grass fence. Without fail, every house had a pit latrine nearby. Riots and fights were rare because I chose an elderly man who was meek to look after the laborers.

During rainy season, there was much cultivation too. We were growing maize, cowpeas, beans, groundnuts, ground peas, elephant grass, ordinary grass and Irish potatoes. The maize was mainly for feeding the cattle and other domestic animals. I was making dry season food using the maize before

ng'amba ndimafukula ndi kudyetsa ng'ombe. Dzina lake la chakudyachi ndi sayileji.

Chimanga china ndimachisiya kuti chidzakhwime nkudya monodokwa mpaka kukolola. Ndimakonza nkhomwe ndi masindwi ake omwe ndithiramo chimanga, khobwe, nsawa, nzama ndi nyemba. Udzu uja ndimaudula ndikusunga pamalo abwino kutinso nthawi ya ng'amba ng'ombe ndi ziweto zina zidzadye. Dzina lake timati he.

Nthawi ya dzinja timawona tizilombo tosiyanasiyana. Todyedwa ndi tosadyedwa. Todyedwa ndi monga: inswa, mafufufute (nyamu) ndi nkhanu. Tosadyedwa ndi monga: mifojwe, nyerere, bongololo, nkho, kamba (fulu), chule ndi linthumbwi.

Mtedza wa mtundu wa chilimbana ndi kalisere sumalola kwenikweni pafama imeneyi. Umachuluka mandolo, makamaka nthaka yake sinali yabwino chifukwanso cha mchenga wochuluka. Mvula ya mvumbi ndi matalala ndi imene akonda kugwa dera limenelo. Ndipo mitsinje yambiri imakhuta koti kuwoloka kunali kovuta kotero kuti anthu ena akati achite khama amatengedwa ndi madzi kapena kudyedwa ndi ng'ona.

Panali wantchito wina amene anali wamatsenga. Pamwezi uli wonse pamapezeka kuti ndimamulipira kawiri kapena katatu. Anali ndi makhwaladi a chidima kotero kuti ndinavutika kamamulipira ndalama zanga za pamwezi chifukwa zimaperewera, koma osamuziwa konse. Maloto anga osandiuzapo za munthu ameneyu ndipo ndinali kuzaza ndi kukalipa mumtima. Munthu wachiwembu otereyi anandidandaulitsa mpaka zaka zinayi.

Nditakwatira mkazi dzina lake Madalitso m'mudzi mwa Chitseko, anali mkazi wachangu. (Ndikachoka kumunda kudzabindikira muofesi mwanga osalephera kupeza wavundikira nsima, ndati: "mwamuna usamamuwone pankhope, nkhope

it was ripe, just as it started flowering, with corn silk and cobs still tender. I was digging a big hole and cutting the maize in pieces and burying it in the big hole. During the dry season I was taking it out of the pit and feeding the cattle. The name of the feed was silage.

Some of the maize was left to get ripe and we ate it as green maize and some we harvested. I was making granaries and their roofs, and into the granaries we put the maize, cowpeas, groundnuts, ground peas, and beans. The ordinary grass was cut in pieces and put in a good place so that in the dry season the livestock should eat. The name of such a feed was hay.

During the wet season we were seeing different kinds of creatures, edible and not edible. Some edible ones were: white ants, termites and crabs. Inedible ones were big black ants, ordinary ants, centipedes, snails, tortoises, frogs and "linthumbwi" (a kind of ant).

Groundnuts of the "Chalimbana" variety (big groundnuts) and "kalisere" (small type groundnuts) didn't grow well at this estate. They were mostly tender groundnuts. The soil was not good because it had much sand. Hail-storm and non-stop rain was the most common type of rain in this area. And many rivers were flooding so that crossing them was difficult and if any persons persisted in crossing they were drowned (or taken) by the floods or eaten by crocodiles.

There was one worker who was a magician. Every month it was found that I was paying him for two or three months. He had the medicine which made me not know that I had paid him and would even pay him my own money from my own salary because there was a shortage, without knowing he was the one doing such things. I could not dream about this man and I was annoyed and angry in my heart. This tricky man made me complain for four years.

sisintha koma kumimba"). Mlongo wake wa Madalitso dzina lake Sinjani, ndimamlemba ntchito yoyendetsa thalakitala. Nthawi yina ndinamudandaulira za matsenga amene anali pantchitopo, ndipo iye anati tidzapita kwa sing'anga wina dzina lake Puludzu, amene angandithandize, Sinjani nayenso amafuna mankhwala amangolomera (katuku) kuti azipambana pomenyana ndi anzake.

Tinanyamuka tsiku lachinayi ulendo wa mitunda makumi atatu panjirga. Tinapeza mtsinje dzina lake Bua, ndipo mulamu uja powoloka anaterereka ataponda mwala wondere nkugwa koma njinga idayandama ine nkuitenga. Sinjani anali odziwa dera (kusambira), anakhupukanso mosavutika. Koma poti inali nthawi ya mawa kuli chisanu, anali okongwa (ozizidwa). Tinakwera njinga zathu ndikuyambaso ulendo. Nkhanga zili cheeeee kulira, kudali kumawa kwambiri dzuwa lisanatuluke, m'phiri mukumveka malubza a munthu akudula mtengo. Titabzola pachigayo cha mtengo, tinafunsa mayi wina amene amatonthoza mwana ngati kwa aPuludzu tayandiikira, iye anati: mwafika tsopano. Titapitirira pang'ono chilere cha nsawa tinapeza anthu akuwoka mbande za fodya, ndinati ine kwa anthuwo: "Safunsa adalowera njira ya kumanda", kodi nyumba ya Puludzu ndi yiti? Anthu aja anati iyo! Mulamu uja atatopa tsopano.

Tinawodira kwa amayi amene tinawapeza akupala nsomba za matumbi makwa (mamba). Ndatikhazika pachikopa cha insa. Ndinafunsa ngati aPuludzu alipo ndipo anati alipo ali kuseri kwa nyumba ndipo akhala pasaka, akupala nsungwi za licherero. Titazungulira kuseri kwa nyumba ija tinapeza kamphonda ka galu katsopano kali manthongo khathikha, katagona pasaka.

Tinabwerera kwa amayi omwe aja ndipo mulamu uja anati: "Amuna anu palibe pasaka paja mumanenapa, pali kamphonda ka galu kobadwa tere. Mayi anakalipa

I married a woman called Madilitso (meaning "blessed") in Chitseko village; she was a hard-working woman. (When I was coming from the farm to confine myself in my office she wouldn't fail to come with 'nsima' covered and she'd say: "Don't look at your husband on the face, the face does not change but the stomach.") The brother of Madilitso whose name was Sinjani (meaning "you pound") was employed as a tractor driver. At one time I complained to him about the magician at the estate; he suggested that we should go and visit one witch doctor whose name was Puludzu; he could help me, and Sinjani, too, wanted medicine for strength so that he could win any fight with anyone.

We left on Thursday on our bicycles for a 30 mile journey. We came to a river called Bua, and my brother-in-law, as he was crossing it, slipped when he stepped on a mossy stone and fell but the bicycle floated and I got it out. Sinjani knew how to swim. He crossed without difficulties. But since it was in the early cold morning hours, he shivered with cold. We rode our bicycles and restarted our journey. Guinea fowl still could be heard. It was very early morning before the sun rose; in the hills we could hear echoes of someone cutting trees. We passed the grinding mill of Mr. Mtengo. We asked another woman who was quieting a child if we were near Puludzu's home. She said: "You have now arrived." Soon after passing a groundnut garden we found people transplanting tobacco seedlings. I said to the people: "A person who does not ask followed a path to the graveyard. Which is Mr. Puludzu's house?" The people said, "That one." My brother-in-law was tired now.

We announced our presence to the woman whom we found taking scales off of fresh fish. She told us to sit on an antelope skin. I asked her if

kwambiri ndikutitengeranso kuseri kuja kwa nyumba. Tinawona a Puludzu ali pasaka akupala nsungwi ndipo anati "kodi ndi galu uyu"? Ine mwachidule ndinangopepesa ndi ndalama.

Anatilonjera aPuludzu aja ndi mawu awa amene anandidabwitsa: "Inu ndinu a Chiwala ndipo mukufuna mankhwala ochotsa chidima. Pali munthu wina ndikuwuzani dzina lake amene amalandira ndalama kwa inu kawiri kapena katatu pamwezi uli onse mwa matsenga ndi chidima. Ndikuthandizani, ndipo dzina lake ndi Tembo koma simukamuchotsa ntchito chifukwa zilipo zimene ndikuchitireni ine kuti mtima wanu waukali ufe. Mulamu uja kuti aziyankhula; Sing'anga anati iwe tonthola. "Iwe ndiwe Sinjani dzina lako. Zimene ukufuna ndikupatsa, ukuti ukufuna ndikutemere mankhwala a katukwi. Ndikudandaulira kwambiri, kodi uli ndi ng'ombe kapena mbuzi zoti uzikalipira milandu yomenya anthu? Chifukwa ndi milandu mukuyiputayi. Chabwino mwana akalilira fupa mpatse," idatero sing'anga.

Ine anandipatsa mankhwala oti ndikasamba kumaso tsiku la malipiro ndipo chiponda mtengo ndinapereka K1.00. Mulamu wanga anamulamula K3.00 koma anamulowetsa m'nyumba ya ndendera gulubidi. Nati; ndikutsekera muno chimene uchiwone umenyane nacho uchikanikizire pansu ndipo iwe udzakhala munthu omenya ngakhale mudzi wathunthu.

Atamutsekera, sipadapite mphindi, Mulamu uja anayamba kulira ndi kumenya chitseko kolimba kotero kuti Sing'anga uja anamva chisoni ndikumutsekulira. Anangoti buli kuthawa, kusiya njinga ndi ndalama zomwe. Ndinaseka kwambiri mpaka misozi mbwembwembwe.

Ndinatsazika nditatenga njinga ziwiri, yina nditakwera yina ndikumayendetsa. Nditacheukira kumawa ndinawona utaleza Kenaka ndinampeza Sinjani ali wefuwefu.

Mr. Puludzu was near and she said that he was, and that he was behind the house and was sitting on a sack, smoothing the bamboo strips with which he could make a winnower. When we went behind the house to where the man was supposed to be, we found a new puppy with dried tears lying on the sack.

We returned to where the woman was and my brother-in-law said: "Your husband is not on the sack you talked about; there is a newly born puppy." The woman was annoyed and she took us back to the same place, behind the house. We saw Mr. Puludzu seated on the sack smoothing the bamboo strips and she asked, "Is this a dog?" In short, I just apologized by giving money.

Mr. Puludzu welcomed us with the following words which astonished me: "You are Mr. Chiwala and you want medicine which can remove dark magic. There is a certain person (I will tell you his name) who receives wages from you twice or thrice every month through dark magic. I will help you, and his name is Tembo but you won't sack him because I will do certain things to cool your angry heart." So the brother-in-law was about to talk when the witch doctor told him to shut up. "You are Sinjani. What you want I will give you. You want tattoos for strength. I pity you very much. Have you cattle or goats to pay in court for beating people? Because these are cases you are begging. All right, when a child cries for a bone give it to him," said the witch doctor.

He gave me medicine which I would put in the water for washing my face on pay day and I paid an initial fee amounting K1.00. My brother-in-law was charged K3.00, but he took him into the round house. He said, "I will lock you here, whatever you see fight against it, press it on to the floor and it will turn into a talisman. Then give me the talisman, after which I will make some tattoos on you and you will be able to beat even the whole village."

Ine pomfunse anati: Mulamu! ndikanafa ine lero. Chinjoka cha mtundu wa songo chinandizingiza mwakuti ine ndimalephera kupuma. Iyete Sinjani mkazi, wake dzina lake ndi Chimwemwe, ndipo anati kwa ine: Chimwemwe akadandiiwala pano nditafa. Za ndalama zija K3:00 sanakumbutsenso.

Tinafika mudzi wina wa Mwanaalirenji, tira tsika njinga zathu kuti timwe adzi. Munthu uyu analidi ndi zinthu zambiri monga: Nkhokwe ya chiveza, mapira, misale, minkhaka, kayimbi, mavwende, nzimbe, maungu, chinangwa, phwetekere, mitengo ya mapapaya, peyala ndi ya mango a mtundu wa boloma. Ndipo chimanganso cha khwimbi anali nacho.

Titafika kufama, ndinasunga chinsinsi osauza munthu aliyense kupatula mkazi wanga mpaka tsiku la malipiro, ndinasamba kumaso mankhwala aja ndikupita kuofesi kulipira mmodzimodzi. Koma ntchito inayenda bwino lomwe opanda woti walandira kawiri kaya katatu ngati kale. Malipira anga sindidawakhudze monga ndimachitira kale. Tembo uja kumamuwona ndikusangalala naye bwino lomwe koma opanda kanthu kali konse komuchita.

---



When he was locked in, a minute did not pass before the brother-in-law began crying and beating the door so much that the witch doctor felt pity for him and opened the door for him. He just came out and ran away, leaving the bicycle and the money. I laughed so much that tears came to my eyes.

I bid farewell and took the two bicycles; I rode on one bicycle and just pushed the other. When I turned to the east I saw a rainbow and I cycled for four miles, but without seeing the brother-in-law. Later I found Sinjani panting. When I questioned him he said: "Brother-in-law, I would have died today. A snake of the 'songo' type wound itself around me so that I could hardly breathe." The wife of Sinjani was Chimwemwe and he said: "Chimwemwe would have forgotten me now if I died." He never reminded me about the K3.00.

When we reached a village called Mwanaalilenji, we got off the bicycle for we wanted to drink water. This person of course had a lot of things like granaries of 'chibweza', millet, 'missale', cucumber, 'kanyimbi', watermelon, sugar cane, pumpkins, cassava, tomatoes, paw-paw trees, pear, and mango trees of the big type. And he had also maize which had stayed in the granaries for two years.

When we reached the farm (estate) I kept everything a secret without telling any other person except my wife till pay day. I washed my face using the water in which the medicine was soaked and went to the office to pay (the men) one by one. But everything went on smoothly without any person receiving two or three wages as previously. I never used part of my salary to pay for the balance as I used to do previously. I could see Tembo, and I was happy with him without doing anything to him.

## E. NYAMA ZA M'NKHALANGO

Anthu ochokera kudziko lonse la pansi amafika ku Afilika kudzaona nyama za m'nkhalango. Palibe kontinenti ina imene ili ndi nyama zosiyanasiyana chonchi. Kuti uone mitundu ya nyama zosaoneka kawirikawiri uyenera kukayenda kunkhalango zosungira nyama, kumene nyama zimangodziyendera ndipo sizingaphedwe. Nyama zambiri zazing'ono monga anyani ndi akalulu, zimakhala m'thengo, kunja kwa nkhalango zosungira nyamazi.

Nyama zimene zimadya zomera kawirikawiri zimakhala pamodzi m'magulu. Paphiri la thyatha la Nyika pali misambi yaikulu ya ntchefu ndi mbidzi. Njovu ndi nyama yaikulu kwabasi kuposa nyama zina zonse. Kuli misambi ya njovu kumalo osungira nyama ku Kasungu ndi Nkhotakota. Nyama zina zodziwika zimene zimadya zomera ndi njati, mbawala, gwape, njiri, ndi mvuu.

Nyama zina zimakhala moyo pakudya nyama zinzawo, zimene zimazisaka ndi kuzipha. Mkango ndi nyama yaikulu kwabasi mwa izi; uli ndi mphamvu kwambiri kotero kuto palibe nyama ina ingaupute. Nyalugwe amasaka usiku wokha, ndipo amagona malo obisala masana. Nyama zina zodziwika zimene zimadza nyama zinzawo ndi fisi ndi nkhandwe. Ng'ona imakhala m'madzi ndipo imadza nsomba.

Muli mitundu ya njoka makumi anayi muno in'Malawi. Njoka zimadya abuluzi, mbalame ndi tizirombo tating'onoting'ono. Zokhazo zimene zili zodziwika ndi zaululu ndi mamba, mphiri ndi mbobo. Njoka zambiri, mwachitsanzo chakusa, siziluma anthu. Yaikulu kuposa zonse ndi nsato, imene nthawi zina imatalika kuposa mapazi khumi.

## WILDLIFE

People from all over the world travel to Africa to see the wild animals. No other continent has such a variety of animals. In order to see the rarer kinds you must visit a game reserve, where the animals run free and cannot be killed. Many smaller animals, such as baboons (anyani) and hares (akalulu), live in the woodlands outside the game reserves.

Animals that eat plants usually live together in herds. On the Nyika Plateau there are large herds of eland (ntchefu) and zebra (mbidzi). The elephant (njovu) is the largest of all animals. There are herds of elephant in the Kasungu and Nkhotakota Game Reserves. Other common animals that live on plants are the buffalo (njati), the bushbuck (m̂awala), the duiker (gwape), the warthog (njiri) and the hippopotamus (mvuu).

Some animals live by eating the flesh of other animals, which they hunt and kill. The lion (mkango) is the greatest of these; he is so strong that no other animal will attack him. The leopard (nyalugwe) hunts only by night, and lies in hiding during the day. Other common animals that eat flesh are the hyena (fisi) and the jackal (nkhandwe). The crocodile (ng'ona) lives in the water and eats fish.

There are more than forty kinds of snakes in Malaŵi. Snakes eat lizards (abuluzi), birds and insects. The only common ones that are poisonous are the cobra (mamba), the puff-adder (m̂phiri) and the tree-snake (mbobo). Most snakes, for example the house-snake (chakusa), are harmless to man. The largest is the python (nsato), which is sometimes over ten feet long.

## EXERCISES

A. Answer the following question:

1. Pali misambi ya mbidzi pati?
2. Nyama yaikulu kuposa zonse ndi iti?
3. Anjati amadya chiyani?
4. Anyalugwe amasaka liti?
5. M'Malawi muli mitundu ya njoka iti?

B. Fill in the blanks with the appropriate vocabulary item in parentheses:

(m'nkhalango, zomera, mkango, misambi, mamba, njovu)

1. Pali \_\_\_\_\_ yaikulu ya ntchefu ndi mbidzi.
2. Mvuu ndi nyama imene imadya \_\_\_\_\_.
3. \_\_\_\_\_ zimakhala ku Kasungu.
4. Njoka ziwiri za ululu ndi \_\_\_\_\_ ndi \_\_\_\_\_.
5. Nyama yaikulu kuposa zonse zimene zimadya nyama ndi \_\_\_\_\_.

C. Ask each other questions about the appearance of animals:

Nyama yonenepa ndi iti? - Mvuu ndi yonenepa.

Nyama imene ili ndi makutu aakulu ndi iti? \_\_\_\_\_

Nyama imene ili yoyera ndi yakuda ndi iti? \_\_\_\_\_

etc.

ICHO NCHIYANI?



## 1. CHIFUKWA CHIMENE NKHANGA ILI NDI TSITSI PAMUTU PAKE

Panali munthu wamwamuna amene tsiku lina anapita kukasada ndi galu wake. Tsiku lomwelo mmodzi wa anansi ake ahamwalira mwadzidzidzi, koma popeza iye sanadziwe izi, anapitiriza kusaka, Analibe mwayi, koma pamene dzuwa linali pafupi kulowa anapeza gulu la nkhangha, ndipo imodzi inaphedwa. Anaponya mbalame ija paphewa ndipo anayamba kubwerera kumudzi namaganiza duti akafika kusanade. Koma mosadziwa anasokera. Amangoyenda Mozungulirazungulira osaona chizindikiro choti ali pafupi kufika. Pomva njala anakhala pansu kuti akoleze moto ndikuotcha nkhangha ija. Anaganiza zosunga mutu wake kuti akaonetse anansi ake amene mwina sadakakhulupirira zimene akadawauza. Patangopita nthawi pang'ono anapeza njira yopita kumudzi kumene anauzidwa za imfa ya mnansi wake. Linali tsiku lotsiriza la maliro ndipo dzuwa litangotuluka ofedwa onse anali atameta kale. Anawauza nkhanu ya nkhangha ija ndi mmene iye anasokerera. Pamene ena sanakhulupirire zimene amanena anawaonetsa mutu wa nkhangha uja. Koma modabwitsa wina aliyense mutu uja unali ndi tsitsi ngati la munthu. Onse ananjenjemera ndi mantha ndipo kuyambira nthawi imeneyo nkhangha imadzetsa matsoka pokhapokhapo ngati mutu wake awudula ndikuutaya atangoipha mbalameyo.



## WHY THE GUINEA FOWL HAS HAIR ON ITS HEAD

— FROM MBONA AND OTHER STORIES,  
SCHOFFELEERS AND ROSCOE

There was a man who one day went hunting with his dog. On the same day one of his closest kinsmen suddenly died, but since he was not aware of this, he continued hunting. He had not much luck, but toward sunset he came upon a flock of guinea fowl, one of which fell under his arrow. He slung the bird over his shoulder and turned homeward thinking to reach his village before dark. But before he realized it he had lost his way. He kept travelling around in circles without being able to spot a familiar landmark. Feeling hungry, he sat down to light a fire and roast the guinea fowl. The head, however, he decided to keep to show his kinsmen, who otherwise might not believe his story. Soon after, he was able to find his way back to the village, where he was told about his relative's death. It was the final day of the funeral and just after sunrise the heads of the mourners had been shaved. He told them his story about the guinea fowl and how he had got lost. When some did not believe him he produced the fowl's head. But to everybody's surprise the head had grown hair like a human being! All shivered with fear and ever since, the guinea fowl brings misfortune unless its head is cut off and thrown away as soon as the bird is killed.

## 2. MNYAMATA NDI NG'ONA

Kalekale, padali mnyamata amene adakwatira mtsikana wokongola kwa mbiri. Mtsikana samadya nsima. Amadya mazira a ng'ona okha. Tsiku lili lonse mkazi uja, amauza mwamuna wake kuti apite kumtsinje akamutengere mazira a ng'ona. Mwamuna uja adamuza mtsikana uja zakuopsya kwake kwa ng'ona koma iye sadamvere.

Tsiku lina, mnyamata uja, adapita kumtsinje ndi mlamu wake kukatenga mzira a ng'ona. Atafika kumtsinje kuja, adafunafuna kumene kumakhala ng'ona. Adalipeza dzenje la ng'ona ndipo mnyamata uja adalowa kukafuna mazira. Panthawi iyi ng'ona mudalibe mudzenje muja. Idapita kutali kufuna chakudya chake. Mnyamata atalowa kudzenje la ng'ona ija, adasiya mlamu wake pabwalo kuti amudziwitse ng'ona ikamabwera.

Patapita nthawi pang'ono, ng'ona inayamba kubwera. Idali kubwera ndi utsi kusonyeza ukali wake. Mlamu wa mnyamata uja adayamba kuimba nyimbo kumuchenjeza zakubwera kwa ng'ona.

Mmodzi: Mlamu, mlamu chili nkubwera chalirima.

Onse: Dangula matete.

Mmodzi: Chibwera ndi utsi chalirima.

Onse: Dangula matete.

Mnyamata uja atamva kuimba, anadziwa kuti ng'ona idaali nkubwera. Adatenga mazira anayi mofulumira. Adathawa kupita kumudzi ndipo mkazi wake adakondwera kwambiri. Adaphika mazira aja ndikudya ndi chimwemwe.

M'mawa kutacha, mtsikana uja adauza mwamuna wake kuti apitenso kumtsinje akamutengenso mazira. Mnyamata uja adapita kumtsinje ndi mlamu wake. Atafika, mnyamata adalowanso kudzenje la ng'ona kuti atenge mazira.



## THE BOY AND THE CROCODILE

BY H.Y. MATECHE

A long time ago, there was a boy who married a very beautiful girl. The girl never ate 'nsima'. She liked crocodile eggs best. Everyday, the girl told her husband to go down to the river to fetch the eggs. Although the boy explained to her how dangerous the crocodile was, she wouldn't listen. So everyday the boy went to the river to fetch the eggs.

One day, the boy went down to the river with his brother-in-law as usual. They searched for places where the crocodiles lived. When they had found their holes, he entered it. His brother-in-law was left outside to keep watch, for all the crocodiles were not at home. He found four eggs and took all of them. Before he came out of the hole, he heard his brother-in-law singing a song warning of the crocodile's coming. The song went like this:

One: Brother-in-law, brother-in-law, it's coming very fast.

All: Dangula matete chalirima.

One: It is coming with smoke and flames of fire.


All: Dangula matete chalirima.

When the boy heard this song, he knew that the crocodile was coming, so he went out of the hole very quickly and ran home. His wife was very pleased when she saw the eggs. She cooked them and had a delicious meal.

The following day, the girl told her husband to go down to the river to fetch some more crocodile eggs. The boy went to the river with his brother-in-law. They looked around along the bank where the crocodiles had their eggs. They found a hole full of eggs. The boy entered it to

Mlamu wake adayambanso kuimba nyimbo kumuchenjeza kuti ng'ono idaali kubwera. Mnyamata asanatuluke kudzenje, ng'ona idafika, ndi kulowa kumalo ake. Mwatsoka, idawona mnyamata atatenga mazira ake. Ng'ona idakalipa, ndipo idagwira mnyamata uja ndikumupha ndipo idamuduladula. Mlamu wake adathamanga kukanena kumudzi. Anthu atapita kumtsinje kuja, adapeza kuti mnyamata wafa kale.

Mnyamata adafa chifukwa adakwatira mkazi woyipa.



NG'ONA NDI MAZIRA AKE





II. NKHANI ZISANU\*

- A. KULENGEDWA KWA KAPHIRINTIWA  
'THE CREATION MYTH OF KAPHIRINTIWA'
- B. NAMDZ'AMBE WA NYANGA NDI CHI AMBI CHA MOYO  
'THE HORNED CHAMELEON AND THE ORIGIN OF LIFE'
- C. CHIYAMBI CHA NYANJA YA CHILWA  
'THE ORIGIN OF LAKE CHILWA'
- D. M'MENE KHATE LINABWERERA 'ADZIKO LA PANSI  
'HOW LEPROSY CAME INTO THE WORLD'
- E. CHIYAMBI CHA NYAU  
'THE ORIGIN OF THE NYAU'

\* We are grateful to Prof. J.M. Schoffeleers and Prof. A.A. Roscoe for permission to use their English versions of these stories which will appear in a book entitled Mbona and Other Stories . Cambridge University Press, (expected) 1981.

## A. KULENGEDWA KWA KAPHIRINTIWA

Poyamba kunali Chauta ndi dziko la pansi. Chauta amakhala mulengalenga. Pansi pake panali dziko la pansi, lopanda madzi ndipo lopanda zinthu za moyo.

Tsiku lina mitambo yakuda inawunjikana ndi kuphimba mulengalenga. Ching'aning'ani chinang'anima ndipo kugunda kwa mabingu kumanveka m'mwamba.

Mulengalenga munatsekula ndipo kunatsika Chauta, mwamuna woyamba ndi mkazi, ndipo nyama zonse, mvula ikudza.

Anafikira pa Kaphirintiwa, kaphiri ka pamwamba pathyathyatha, m'mapiri a Dzalanyama. Kenaka malo amene anafikira anasanduka mwala, ndipo mapazi, ndi njira za nyama zambiri, zitha kuoneka pamwalapa mpaka lero. Mapazi a mwamuna uja ndi akulu kuposa a mkazi uja, ndipo ungaonenso modinda khasu dengu lowulutsira mbewu, ndi ntongo.

Zomera ndi mitengo zinamera padziko la pansi ndikubala zakudya zambiri, ndipo Chiuta, anthu ndi nyama anakhalira pamodzi mokondwa ndi anapanga moto woyamba.

Tsiku lina munthu wa mwamuna uja amasewera ndi timitengo tiwiri, kena kofewa ndipo kena kolimba. Anatipekesa pamodzi ndipo mwangozi anapanga moto woyamba.

Aliyense adamuza kuti asiye, koma sanaw mvere. Udzu wonse unapsya ndipo kunali chisokonero chachikulu.

Mkazi mwa nyamazo galu ndi mbuzi zinathawira kwa munthu uja kuti aziteteze; koma njovu, mkango, ndi nyama zina zinathawa zitakwiya ndi munthu ameneyu.

## THE CREATION MYTH OF KAPHIRINTIWA

In the beginning there was Chiuta (God) and the earth. Chiuta lived in the sky. Below him was the earth, waterless and without life.

One day dark clouds built up and covered the sky. Lightening flashed and claps of thunder rent the air.

The sky opened and down came Chiuta, the first man and woman, and all the animals in a shower of rain.

They landed on Kaphirintiwa, a flat-topped hill in the mountains of Dzalanyama. Afterwards the ground where they landed turned to rock and the footprints, and the tracks of many animals, can be seen on the rock to this day. The man's footprints are larger than the woman's and you can see the two imprints of a hoe, a winnowing basket, and a mortar.

Plants and trees grew on the earth, yielding abundant food, and God, man and the animals lived together in happiness and peace.

One day man was playing with two sticks, a soft one and a hard one. He twirled them together and by accident invented fire.

Everybody warned him to stop, but he would not listen. The grassland was set alight and there was a great confusion.

Among the animals the dog and the goat ran to man for protection; but the elephant, the lion, and their companions ran away full of rage against man.

The chameleon escaped by climbing to the top of a tree. He called to God to follow him, but Chiuta answered that he was too old to climb. When the spider heard this he spun a fine thread and lifted God up on high.

Nadzikambe anathawa pokwera pamwamba pamtengo. Anaitana Chauta kuti amsate, koma Chauta anamuyankha kuti sakanatha kukwera popeza anali wokalamba kwambiri. Pamene Kangaude adamva izi anapota chingwe cha thonje labwino ndi kukokera Chauta uja kumwamba.

Choncho Chauta anachotsedwa padziko la pansi chifukwa cha zochita za munthu ndipo pamene anakwera kumwamba ananena kuti kuyambira nthawi imeneyo munthu ayenera kufa ndi kupita kumwamba kukakhala naye.



So God was driven from the earth by the wickedness of man and as he ascended into the sky he pronounced that henceforth man must die and join him in the heavens.

## B. NAMDZIKAMBE WA NYANGA NDI CHIYAMBI CHA MOYO

Kalekale namdzikambe wa nyanga anali yekha wa moyo padziko la pansi. Poyamba anali wokondwa, namayenda uku ndi uku, namasintha kaonekedwe pakhungu lake pamene afika patsamba kapena duwa lokongola; koma patapita nthawi anapukwa ndipo amafuna wina wocheza naye. Anafuna m'mapiri ndi m'madambo koma sanapeze wina aliyense. Kumadzulo ndithu ankakhala mumtengo ndi kumayitana, namakhulupirira kuti wina adzamva liu lake.

Tsiku lina anaona mtengo wabwino, wotalika kuposa ina yonse. Anaukwera nakhala mbali imene zipatso zake zinali zozuna nazidya mokwamila tulo tofa nato tisanamfikire, mkati mwausiku mphepo inayamba kuomba mpaka inakhala mkuntho. Nthambi za mitengo, zimene poyamba zimangogwederera pang'ono, zinayamba kuvina mwamisala mumkuntho umenewu. Namdzikambe adaali mtulo kotero kuti sanadziwe zimene zimachitika, koma kamphepo kamene kadangobwera mwadzidzidzi kanamugwedeza m'nthambi muja. Anagwera pamwala umene unali pansi pake, ndi kuphulika, ndi kufa.

Chinthu china chodabwitsa tsopano chinachitika. Kuchokera m'thupi la namdzikambe lija munafuma nyama zamitundumitundu ndi tizirombo timene timasambira, zinthu zimene zimauluka, ndi zonse zimene zimayenda padziko la pansi. Zolengedwa zazikulu ndi zazing'ono zomwe zinatuluka m'thupi la namdzikambe mondondoza. Potsirizira kunabwera munthu.

Pazolengedwa zonse zija munthu ndiye anali wochenjera kwambiri. Atangodziwa izi anafuna kuti zonse zija zidzimvera iye. Njira yabwino yoyambira, iye anaganiza, inali kupa'sa nyama ili yonse dzina kuti adzizitanira. Analibe nthawi yochitira izi iye yekha, choncho anaitana nyama imene inali pafupi naye, naiuza kuti ipite panja, itchule dzina

## THE HORNED CHAMELEON AND THE ORIGIN OF LIFE

Long, long ago the horned chameleon was the only living creature on earth. He was happy at first, going from place to place, changing the color of his skin whenever he came across some beautiful leaf or flower; but as time went on he became lonely and longed for a companion. He searched in the hills and in the valleys but found none. In the evening he used to sit in a tree and call, hoping someone would hear his voice.

One day he saw a fine tree, taller than all the others. He climbed to where the fruit was delicious and he ate and ate to his heart's content before falling into a deep sleep. In the middle of the night the wind started to blow and it blew up into a great storm. The branches, which had swayed lightly in the breeze, danced madly in the grip of the storm. Chameleon was so fast asleep that he did not notice, but a sudden gust shook him from his branch. He fell onto a rock below, burst open, and died.

Something very surprising now happened. Out of the chameleon's body came all kind of animals and insects--things that swim, things that fly, and those that walk on the earth. Creatures great and small came from chameleon's body in an endless stream. And last of all came man.

Of all the creatures man was the cleverest. As soon as he discovered this he wanted to subject all the others to his will. The best way to start, he decided, would be to give every animal a name so that he could call them. He did not have time to do this himself, so he summoned the animal closest to him and told him to go out, name all the animals, and return when he had finished. The animal went and gave every creature a name, but he forgot to name himself.

nyama zonse, ndi kubwerera pamene yatsiriza. Nyama ija inapita ndi kupatsa cholengedwa chili chonse dzina, koma inaiwala kudzitchula dzina.

Kutchula maina kuja kutatha, munthu uja anakonza phwando lalikulu ndi zakudya zambiri naitana nyama zonse. Anaitana maina ndipo nyama ili yonse imaima monyadira ikamva dzina lake. Koma nyama imene imatchula zinzake maina sinaitanidwe chifukwa idaiwala kudzitchula dzina.

Pamene nyama zina zidamva izi zidaseka kwabasi mokweza. Zidaganiza kuti chinali choseketsa kuti amene wavutika ndi kutchula maina anzake aiwale kudzitchula iye mwini. Mokwiya ndi mwamanyazi nyama ija inalira, "Mukuseka ndani? Mukundiyesa ine galu?"

Kuyambira tsiku limenelo aliyense anamuitana ndi dzina limenelo.

Mkati mwa nyama zimene zidabwera paphwando paja pana i namdzikambe wamng'onc wa nyanga, mwana wa mwamuna wa namdzikambe woyamba uja amene adafa. Pamene adaona kuti munthu walanda ulamuliro kuchokera kwa anamdzikambe anakwiya. Adafuna kuti atsutse ndipo anauza onse kuti akhale chete, koma panalibe wina adamumvera. Pamene adayesa kulankhula anzake anamuseka, choncho anatuluka nabwerera ku nkhalango kuja. Kumeneko anakapukwanso monga lidachitira kholo lake, ndipo nchifukwa chake timapeza namdzikambe wa nyanga akuimba mokwiya mumitengo mpaka lero.

When the naming was finished, man arranged a big feast with plenty of food and invited all the animals. He called the roll and each animal rose proudly in answer to his name. But the animal who had named all the others was not called because he had forgotten to name himself.

When the animals heard this they laughed out loud. They thought it very funny that the one who had taken so much trouble over naming the others should have forgotten to name himself. Angry and ashamed the animal cried, "What are you laughing at? Do you take me for a dog?"

And from that day everybody called him by that name.

Among the animals gathered at the feast was a small horned chameleon, a son of the first one who had died. When he saw that man had taken authority away from the chameleons he was angry. He wanted to protest and called for silence, but nobody took any notice of him. When he tried to speak he was shouted down, so he stalked out back to the forest. There he became lonely again like his parent, and that is why we find the horned chameleon singing sadly in the trees to this day.

## C. CHIYAMBI CHA NYANJA YA CHILWA

Tsiku lina madzulo anyamata atatu adaganiza zokwere phiri limene linali lodziwika kwambiri chifukwa cha uchi wake. Kwa zaka zambiri njuchi zinakhala zikumanga zisa zawo m'phanga pafupi ndi pamwamba paphirilo. Aliyense adati kukakhala uchi wambiri kumeneko koma panalibe wina adayesera kupita kukafula njuchizo, kungopatula anyamata atatu olimba mtima.

Anakwera paphiri mpaka paphanga paja ndipo pamenepo anayatsa moto udzu wouma umene anatenhera mkati mwa phangamo ndi kufuikiza njuchi zija kuti zichoke ndi utsi. Pamene anachita izi mnyamata wamkulu paonse aja anadzipereka kulowamo poyamba. Analowa m'phanga muja ndikubwerera patangopita kanthawi pang'ono ndi mphika odzadza ndi uchi. Analowanso kachiwiri ndikubweranso ndi mphika wina. Koma atalowanso kachitatu mphepo yozizira inawomba kuchokera mkati mwa phanga muja. Inawomba mwamphamvu ndi mkokomo popeza umu ndimo mumakhala nsato. Anachita mantha ndipo anayesa kuthawa, natrya mphika wake wa uchi uja pathawa. Koma atangofika pakamwa paphanga paja njoka ija inamugwira ndi kumupha, ndipo anzake awiri aja amene anayesa kumpulumutsa anaphedwanso.

Mdima utayamba ndipo anyamata atatu aja osabwerera kumudzi, anthu anayamba kuchita mantha ndipo anatumiza gulu lonka liwafuna m'mawa limene mfumu adalitsogolera. Pamene gululi linafika paphanga, linapeza matupi atatu a anyamata aja ndi nsato yaikulu itawazungulira. Anakalipa ndi kuyamba kulasa njoka ija ndi mikondo yawo; koma idapha anthu oweregeka isanathaawe ndikutsikara m'munsi mwa phiri lija. Mfumu ija ndi anthu ake anaithamangitsa, uku akunka nayibaya.

## THE ORIGIN OF LAKE CHILWA

One afternoon three young men decided to climb a hill which was famous for its honey. For years bees had been building their nests in a cave near the top. Everybody said there would be plenty of honey there, but nobody dared to go and collect it -- except our three brave youngsters.

They climbed up to the cave and there they set fire to the dried grass which they burnt inside the cave to smoke the bees out. When they had done this the eldest of the three offered to go in first. He went into the cave and came back after a while with a pot full of honey. He went a second time and brought back another pot. But when he went in for the third time an ice cold wind blew from the deepest recesses of the cave. It blew more and more strongly and was accompanied by a horrible hissing noise for this was the home of an enormous python. Fear took hold of him and he tried to run away, dropping his pot of honey as he went. But just as he reached the mouth of the cave the snake caught and killed him, and his two companions who tried to save him were killed too.

When night fell and the three boys had not returned to the village, the people feared the worst and sent out a search party in the morning under the chief's command. When this party reached the cave they found the three bodies with the huge python curled around them. They were angry and began to attack the snake with their spears; but it killed several of the party before it took itself off, slithering down the hill. The chief and his men ran down the hill after it, striking it as they went. But once down in the plain the python turned round and

Koma itafika m'dambo nsato ija inatembenuka ndikutulutsa mphepo ya mphamvu kuchokera m'mphuno zake kotero kuti inapha anthu onse aja kupatula mfumu ija, imene inatetezedwa ndi mphamvu za padera za mankhwala.

Choncho mfumu ija inatsala yokha ndi nsato ija ndipo nkondo yoopsya inayambika pakati pawo. Zochitika pankhondopo zimaveka kutali. Potsiriza mfumu inapambana poilowetsa mkondo wake kukhosi nsato ija. Komanso pakufa nsato ija inadzizunguza pathupi la mfumu ndi kuphwanya mafupa ake kotero kuti onse anafera pamodzi. M'maisa misake, pamene amayi amanka nayang'ana mfumu yawo, sanalipeze thupi lake. M'mawa mwake anapeza dziwe lalikulu limene silinali malo amenewa kuyambira kale. Ndipo dziwe lija linayamba kukula tsiku ndi tsiku, kukulirakulira mpaka onse osatha kuona tsidya lina. Umu ndi m'mene Nyanja ya Chilwa idapangidwira.





let forth from its nostrils a wind so strong that it killed all the men except the chief, who was protected by special powers.

So the chief was left alone with the python and a terrible battle now took place between them. Their moaning and hissing could be heard for miles around. At last the chief succeeded in thrusting his spear deep into the serpent's throat. But with its dying spasm of agony the python curled itself round the body of the chief and crushed his bones so that the two died together.

Next morning, when the women went out looking for their chief, they did not find his body. Instead they found a big pool which had never been there before. And the pool began to grow day after day, bigger and bigger, until they could no longer see to the other side. And that is how Lake Chilwa was formed.

## D. M'MENE KHATE LINABWERERA PADZIKO LAPANSI

Kalēkale kunali atsikana awiri okongola m'mudzi wa pansi padziko. Maina awo anali Tsekanao ndi Chirile. Onse ankafuna kukhala ndi ana, ndipo adamva za mayi wokalamba amene amakhala m'dziko limene linali pamwamba pawo amene akanatha kuwathandiza. Anali wochititsa mantha kumuyang'ana. Anali ndi diso limodzi lokha, koma diso limenelo linali la mphamvu kwambiri kotero kuti likanatha kuona zinthu zimene zinali kutali kwambiri ndiponso kuona zachinsinsi m'mitima ya anthu. Atsikana aja anagwirizana kuti Tsekanao apite poyamba kukaonana ndi mayi wokalambayu pa vuto lawo.

Ali m'njira yopita kudziko limene linali pamwambwa pawo Tsekanao poyamba anakomana ndi nyerere zazing'onŋ zimere zidampempha kuti ziyende naye pamodzi. Iye mwaulemu anavomera ndipo kuyambira pamenepe gulu laling'ono la nyerere linayamba kuyenda naye pamodzi. Akangaude nawo analowanso m'gulumo, ndi nkono, ndipo iye onsewo anawalandira, ndipo potsiriza gulu la anagogomola. Onse anayenda mosangalala mpaka anafika pamtsinje umene udalemba malire a pansi pa dziko ndi dziko la pamwambwa, ndipo, mosayembekezera, anapeza, mtsinje uja utadzaza ndipo wakuya kwambiri kotero kuti sankatha kuwoloka. Koma kangaude, monga munthu wogwiragwira, anakoza ulalo ndipo gulu lonse lija linawoloka bwinobwino. Posakhaliitsa anafika panyumba ya mayi wa diso limodzi uja amene anali wokalamba ndipo Tsekanao anamuza zimene anadzera. Poyamba, anauzidwa, kuti ayenera kugwira ntchito. Mayi wokalamba uja anabweretsa mawere, mchewere, ndi "sesame", zonse zinasokanirana ndi mfumbi ndi mchenga. Iye adafuna kuti zikhale zopanda mfumbi ndi kuziika m'magulumagulu ndipo ndikuziperera pazokha.

## HOW LEPROSY CAME INTO THE WORLD

Once upon a time there lived two beautiful girls in a village of the underworld. Their names were Tsekanao and Chirile. Both longed to have children, and they had heard of an old woman in the world above who might be able to help them. She was horrible to look at. She only had one eye, but that eye was so powerful that it could distinguish things at a great distance and see the secrets in people's hearts. The girls decided that Tsekanao should go first and tell the old woman about their problem.

On her way to the world above Tsekanao first met little ants who asked her if they could travel with her. She kindly said yes and from then on a small army of ants became her constant companions. Spiders too joined the party, and snails, and she welcomed them all, and finally a family of woodpeckers. They all travelled merrily along until they reached the river which divided the underworld from the world above, and, to their dismay, they found the river was in flood and too deep to be forded. But the spiders, practical as ever, made a bridge and the party was able to cross in safety. Presently they reached the house of the one-eyed woman and Tsekanao made her wish known. First, she was told, she must render a service. The old woman brought out a basketful of finger millet, bullrush millet, and sesame, all mixed together with dust and sand. She wanted the grains all cleaned and sorted out and pounded separately. But there was no pounding pestle.

Koma mpheru panalibe. Tsekanao sanatsutse koma mwachisangalalo anapita ndi gulu lake lija kukamtsinje kamene kanali pafupi ndi kumene onse adayamba kugwira ntchito ija atangofika. Nyerere zinatola tinjene tating'onoting'ono, akangaude amaluka madengu, ndipo nkho zinatenga madengu aja kumisana kwawo ndi kukaika pambali pamtsinje kumene anagogomola adayamba kupera. Pasanapite nthawi ntchito yonse inatha ndipo anayamba kubwerera kunyumba kwa mayi uja ndi madengu atatu odzaza ndi ufa wabwino kwambiri. Iye anakondwera ndipo anawauza kuti agone komweko m'nyumba yake ija mpaka mawa.

M'mawa kutacha Tsekanao amauonetsa nzera wa mipika ina inali yatsopano ndipo yokongoletsedwa bwino, koma ina inali yakale ndi yowiritsira kale ntchito. Mayi wokalamba uja anamuza Tsekanao kuti atenge mpaka umodzi wakale, ndipo mtsinje umene ulemba malire amayiko awiri aja. Tsekanao anafumira kuwerera ndipo atawoloka mtsinje uja bwinobwino anatsegula mipika uja ndipo anapeza kuti munali mwana wonenepa ndi wokongola.


Aliyense a asirira mwana wa Tsekanao, ndipo mnzake Chirile anali ndi nsanje, choncno anaganiza zopita nthawi yomweyo kukaona mayi wokalamba uja naye. Koma pamene Chirile anakomana ndi nyerere anakana kumkera nazo limodzi popeza adafumira kwambiri. Zinachitika chimodzimodzi pamene anakomana ndi akangaude, nkho, ndiponso anagogomola. Mwamwayi wake madzi a pamtsinje uja anali atapita (atashapa) ndipo anawoloka mosavuta. Koma atafika kunyumba ya nzimayi wokalamba uja anapatsidwa njere zija zosokonezeka ndi mchenga ndi mfumbi kuti azipatulapatule, anatenga dengi kupita nalo kukamtsinje koma analephera kuzipatulapatula.

Tsekanao did not protest but cheerfully led her party to a nearby stream where they all set to work at once. The ants sorted out the little grains, the spiders wove baskets, and the snails carried the baskets on their backs to the river bank where the woodpeckers did the pounding. Before long the work was finished and they made their way back to the woman's house with three baskets full of the finest flour. She was delighted and bade them spend the night in her house.

Next morning Tsekanao was shown a row of pots, some of which were new and beautifully ornamented, while others were old and worn with use. The old woman suggested that Tsekanao take one of the old pots, and the young girl accepted this advice. She was told not to open the pot until she had crossed the river which flows on the border between the two worlds. Tsekanao hurried on her way and once safely on the other side she opened the pot and found in it a fat and lovely baby.

Everyone admired Tsekanao's baby, and her friend Chirile was jealous, so she decided to go at once and see the old woman too. But when Chirile met the ants she refused to let them travel with her as she was in too much of a hurry. So it was with the spiders, the snails, and the woodpeckers. Luckily for her the waters of the river had gone down and she could cross it. But when she got to the old woman's house and was given the grains mixed with sand and dust to sort out, she took the basket to the stream but could not do it.

Kutada anatenga dengu lija nabwerera nalo kunyumba kuja monga m'mene iye analirandirira. Mayi wokalamba uja anamuza kuti agone pomwepo ndipo kummaŵa anamuonetsa nzera wa miphika. Koma Chirile anaumirira, ngakhale mayi wokalamba uja anamulangiza, kusankha mphika wowala kwambiri ndipo umene unakongoletsedwa kuposa ina yonse. Atawoloka mtsinje uja anadikira mpaka abwenzi ake ndi anasi ake atafika kuti asirire chimene anakatenga asaratsegule mphika uja. Koma taonani! Pamene anatsegula anapeza kuti munali mwana woipa ndi wazilonda ndi zotupatupa thupi lake lonse. Umo ndiye m'mene khate linabwerera padziko la pansi lino. Kusamvera malangizo w' akulu kumabweretsa matsoka.



ATSIKANA AWIRI

When evening fell she took it all back to the house just as she received it. The old woman asked her to stay the night and in the morning showed her a row of pots. But Chirile insisted, against the advice of the old woman, on choosing the shiniest and most beautiful ornamented pot of all. After she had crossed the river she waited until all her friends and neighbors were present to admire what she had brought before she opened the pot. But lo and behold! When she did open it, the pot was found to contain an ugly baby with sores and swellings all over his body. And that is how leprosy came into this world. Neglecting the advice of elders always brings misfortune.

## E. CHIYAMBI CHA NYAU

Masiku akale, makolo atangofika kuchokera ku Kaphirintiwa kunali njala yaikulu. Anthu anali ndi njala mudera lonse ndipo pamene zakudya mnkhokwe zimachepa amayi anaganiza zosunga chakudya chotsala chija kuti iwo ndi ana awo azidya kuti mtundu usathe. Abambo onse anauzidwa kuchoka m'midzi ndi kulakhala ku nkhalango, kudya masamba ndi mizu ndipo ndi zipatso zimene akanazipeza. Panalibe china abambo aja akanachita popeza amayi aja ndiwo anali eni ake enieni a mudzi uja.

Kunayamba kuwonekeratu kuti abambo aja sakanakhala ndi moyo m'nkhalango muja. Anamva njala koopsya mpaka zinthu zinafika poyipa kwambiri. Potsiriza anagwirizana zoti iwo apeze njira yoti apezere gawo lawo la chakudya chimene iwonso anathandiza kuchilima. Wina adapezeka maganizo oti aphe amayi onse aja ndi kuwadya. M'njira imeneyo, iye anati, abambo onse ndi ana adzapulumuka ndipo abambo adzapeza gawo lawo la zakudya zimene zinayenera kukhala zawo. Koma ena anati zoterezi zikanakhala zopusa chifukwa amuna okha akadakhala moyo pakanasoŵa wophika chakudya ndi kusamala ana aja. Atakhala m'nkhalango muja kuyesa kupeza njira ina, mmodzi anayimirira nanena kuti:

"Akulu anga ndi abwenzi, ganizo landifika. ndikuwululireni kuti muone ngati ndi la nzeru kapena lopusa. Amayi watithamangiŵa ife kuti tikhale ngati nyama m'nkhalango. Ichi ndi chinthu cha nkhaza kuchita ndipo tiyenera kuyesa ndi kuwalanga. Ndikuganiza kuti tibwerere kumudzi titadzikhazika ngati nyama. Pamene amayi aja akawona ife tikubwera sakadziwa kuti ndi ife; akaganiza kuti akuputidwa ndi nyama zakuthengo. Iwo akathaŵa mwamatha ndipo ife tikatha kutenga chakudya chimene tikuchisoŵa."



## THE ORIGIN OF THE NYAU

In the olden days, not long after the ancestors had come from Kaphirintiwa, there was a great famine. People were hungry in the land and as the stores of food diminished the women decided to keep what little there was left for themselves and their children so that their line might continue. The men were told to leave the villages and live in the forest, eating leaves and roots and whatever fruit they could find. There was nothing the men could do about it since the women were the rightful owners of the village.

It soon became clear that the men could not survive in the forest. They became steadily hungrier until their condition was desperate. So finally they decided some way must be found for them to get their fair share of the food which they had helped to produce. Someone suggested they should kill all the women and eat them. At least that way, he said, the men and the children would survive and then men would get the share they deserved. But the others pointed out that this would be foolish for if only the men survived, there would be nobody to cook the food and look after the children. While they sat in the forest trying to think of some other solution, one man stood up and said:

"My elders and friends, a thought has just struck me. I will reveal it to you so that you may decide whether it is wise or foolish. The women have condemned us to live like animals in the forest. This was a cruel thing to do and we should try to punish them. I propose that we return to the village disguised as animals. When the women see us coming they will not know that it is us; they will think they are being attacked by wild animals. They will flee in panic and we will be able to take the food we need."

Abambo onse amene analipo anawombera m'manja ganizoi ndikuyamba kugwira ntchito pompo. Adasankha kumanda, m'nkhalango, ngati kogwiria ntchito chifukwa amayi aliyense sakadayesa kufikako ndipo adafuna kuti izi zikhale zachisisi. Amapanga zisudzo zofanana ndi mkango, njovu, ndi nyama zina zambiri, ndipo zisudzozi zimaoneka ngati zirombo zenizeni kotero kuti zimachititsa mantha. Ng'oma zodabwitsa zinapangidwanso, kaliridwe kake kanali kasanamvekenso. Abambo aja anagwira ntchito osatopa usiku ndi usana mpaka sabata yonse ndipo samamvanso njala, kupweteka m'mimba zawo ndiye kumamveka.

Nthawi ya chisisira tsiku adapangana lija amayi amakonza chakudya cha madzulo pamene mwadzidziazi adamva kulira kwa ng'oma kwachirendo ndi kochitsa mantha kuchokera kunkhalango kuja, kumene kunali manda. Anaganiza kuti zinali ng'oma za mizimu ndipo mantha anawagwira. Pamene anayimirira anawona nyama zamitundumitundu kutuluka kunkhalango kuja kumadza kumudzi kuja. Panali chipwirikiti. Amayi anasiya zimene anali kuchita, anatola ana awo, ndikuthawa kuti angafe.

Pamene abambo aja anaputa mudzi uja ndipo, atavalabe ngati nyama, anayamba kuvina mododometsa pamabwalo a nyumba zija. Ng'oma zija zinamveka kuimbidwa mofulumira ndipo mtambo wa pfumbi unakwera pamwamba pamudzi uja.

Amayi, akuonera kuchokera m'malo anabisala aja, anawona kuti nyama zija zimaba zakudya zawo ndipo anachita mantha kuti china sichitsala choti ana awo adye. Anatumiza nthumwi kukapempha nyama zija kuti zisiye china kuti iwo ndi ana awo asafe. Amayi aja anakhulupirira kuti chirangochi chinatumizidwa ndi mizimu chifukwa anachita zankhaza kwa abambo aja; ndipo analonjeza kuti

C

All the men present applauded this idea and set to work at once. They chose the burial place in the forest for their workshop because no woman would ever dare to set foot there and they wanted to keep it secret. They made masks in the likeness of lion, elephant, and many other animals and these masks were so true to life that they were terrifying. Special drums were made too, the sound of which had never been heard before. The men worked tirelessly night and day for a whole week and no longer felt hunger pangs gnawing at their stomachs.

At dusk on the appointed day the women were preparing the evening meal when suddenly they heard a strange and frightening roll of drums coming from the forest where the burial place was. They thought it was the drums of the spirits and fear gripped them. While they stood rooted to the spot they saw all kinds of animals bursting out of the forest and making for the village. There was pandemonium. The women dropped whatever they were doing, grabbed their children, and ran for their lives.

Meanwhile the men invaded the village and, still dressed as animals, started dancing frenziedly in the open space between the huts. The drums throbbed in an ever faster rhythm and clouds of dust rose above the village.

The women, watching from their hiding places, noticed that the animals were stealing their food and became afraid that nothing would be left for their children. So they sent a delegation to plead with the animals to leave something so that they and their families might survive. The women believed that this punishment had been sent by the spirits because they had been cruel to the men; and so they promised always to let the men share their food. The animals, when they heard this, agreed to return to the

adzalola azibambo aja kugawana nawo zakudya zawo. Nyama zija, zitabra izi, zinalola kubwerera kunkhalango kuja, ndipo patangopita nthawi pang'ono amuna aja anabwerera kumudzi kuja kumene anawasamala mwaulemu.

Gule wa nyama anakondwetsa ali yense kotero kuti anaganiza zomavinabe ngakhale pamene njala ija idatha. Ndipo ndi m'mene gule wa nyau adayambira, ndiponso ndi chifukwa chake amavina ndi amuna okha osati amayi.

forest, and a little while later the men came back to the village where they were treated with respect.

The animal dance pleased everyone so much that they decided to keep it even when the famine was over. And that is how the nyau mask society came into being, and that is why it is a society of men and not of women.



478

KUGHIRA NTCHITO

III. NTCHITO 'WORK'

A. MALAWI LERO \* 'MALAWI TODAY'

1. MADZI NDIWO MOYO

'WATER MEANS LIFE'

2. USODZI WA NSOMBA M' MALAWI

'FISHERIES IN MALAWI'

3. ADMARC IMAGULA MBEWU ZA ALIMU

'ADMARC BUYS SMALLHOLDERS' CROPS'

4. AMAYI PANTCHITO YA CHIPANI NDI YA CHITUKUKO

'WOMEN'S ROLE IN PARTY AND DEVELOPMENT'

B. CHAKUDYA CHABWINO CHOYENERA KUPATSA BANJA

'PROVIDING GOOD FOOD FOR THE FAMILY'

C. TECHNICAL VOCABULARY LISTS

D. ENGLISH-CHICHEWA MEDICAL DICTIONARY

\* These texts are adapted from the bilingual Malawi Lero posters printed by the Department of Information in Blantyre, Malawi.

## 1. MADZI NDIWO MOYO

Madzi ndi wofunika kwambiri kwa ife Amalaŵi, popanda madzi, tonsefe sitingakhale ndi moyo.

Tisadalandire ufulu wodzilamulira, ndi anthu a pang'ono amene ankakhala m'matauni a Blantyre, Zomba ndi Lilongwe, amene ankamwa madzi abwino a m'mipope. Kumidzi, anthu ankatunga madzi awo ku tizitsime tosamalika bwino pamene ena anali kukatunga kumitsinje yomwe inali kutali ndi kwao ndiponso kaŵirikaŵiri madzi ake sanali aukhondo.

Pa chifukwa ichi, matenda amene amalefula anthu, sankachoka pakati pao.

Pansi pa utsogoleri wanzeru wa Ngwazi yathu, vuto la madzi aukhondo m'madera a m'midzi lakhala likunka lichepa.

Zitsime mazanamazana aziboola pofuna kuti anthu azimwa madzi abwino, wochokera pansi panthaka, kumidzi ndi kumalo a chitukuko. Zitsimezi amaziŵaka bwino ndi simentu, poopetsa kuti ziŵeto zingakononge pamalopo. Boma lakhalanso likuphunzitsa anthu za ubwino wake womwa madzi aukhondo.

Zokondweretsa zina ndi zoti, pogwiritsa ntchito nzeru za chibadwa-- zoti madzi amalowera kumalo wotsetsereka--Boma lapatsa anthu ake mwaŵi wodzithandiza wokha potukula miyoyo yao.



## WATER MEANS LIFE

Clean water is the life blood of Malawi. Without it, the nation will wither like the crops when no rain falls.

Before independence, clean water was for the privileged few. Only in the colonial suburbs in Blantyre, Zomba and Lilongwe could one get drinking water by turning a tap. In the villages water had to be drawn from unprotected wells or from rivers and streams. Often, the water was far away from where it was needed. Often, too, it was dirty and contaminated.

And impure water led to diseases and parasites that sapped the strength of the people.

Under the Ngwazi's leadership, the problem of water supplies in the rural areas has been tackled with vigor and determination since Independence.

Thousands of boreholes have been drilled to bring clean water from below the surface of the earth to villages and settlement schemes throughout the country. Thousands of wells have been protected by concrete aprons to prevent animals dirtying them. Extensive campaigns have been mounted to teach people the necessity of drinking only clean water.

Even more impressive, by making use of a simple natural law--that water will always flow to the lowest level--the Government has provided the people themselves with a chance to improve dramatically their way of life.

Anthu a m'midzi eni ake akhala akuika mipope m'madera awo, pofuna kuti azimwa madzi aukhondo, mogwirizana ndi a mu Unduna wa za Chitukuko ndi Zosamalira Anthu. Iwowa amawathandiza kubweretsa madzi kuchokera kumadera okwera ndi kufika kumidzi yawo. Anthuwo amagwira ntchitoyi modzithandiza wokha, polumba ngalande modzayalika mipope, yomwe mwina imakhala ya mamailosi angapo. Boma limawathandiza anthuwa, powapatsa alangizi woyang'anira ntchitoyi, zipangizo zake kudzanso mipope.

Pamakhala ntchito ya kalavulagaga pa miyezi yambiri, pofuna kuti anthu ayigwire mogwirizana. Koma malipiro ake amakhala a akulu, chifukwa choti amamwa ndi kuphikira madzi aukhondo a m'mipope.

Gravity-fed rural piped water projects stem from the people. It is they who decide that they would like to have a better water supply. After consultations with Community Development officials, a permanent source of water is found at a level higher than that of the area to be served. The villagers organize themselves to provide labor to dig many miles of trenching for the pipes. The Government provides experts to supervise the work and funds for materials and piping.

It takes many months of hard work and cooperation by the villagers. But the final reward of being able to turn a tap and have clean water for drinking and cooking makes it all worthwhile.

## 2. USODZI WA NSOMBA M'MALAŴI

Chigawo chosapyola theka la dziko lino la Malaŵi ndi madzi a m'nyanja, a m'mitsinje ndi a m'maiwe ndipo dziko la Malaŵi lili ndi nyanja zisanu--ya Malaŵi, ya Malombe, ya Chilwa, ya Chiuta ndiponso ya Kazuni. Palonso mitsinje yambiri koma wodziŵika kwambiri ndi wa Shire umene ndi wokhawo umachokera m'nyanja ya Malaŵi.

Madzi a m'nyanja, a m'mitsinje ndi a m'maiwe ali ndi mitundu yambiri ya nsomba zomwe anthu amazidya ndi kuzigulitsa kotero kuti usodzi wa nsomba ndi wofunika kwambiri m'dziko lino la Malaŵi--njira zakale ndi zatsopano zogwirira nsomba zikuthandiza pogwira nsomba zambiri.

Usodzi umathandiza anthu ambiri mwa njira zosiyanasiyana--pozigwira, pozisunga, pozinyamula, pozigulitsa ndi pozidya. Ndipo khalidwe lachi-dziŵikire la Angelezi lomadya "nsomba ndi mbatata yokazinga" lazika mizu m'Malaŵi.

Nsomba ndi zambiri ndipo zili ndi zofunika zambiri ku matupi athu ndiponso potipatsa chuma. Pa chifukwa ichi a Dipatimenti yoyang'anira za usodzi wa nsomba womwe ali mu Unduna wa za Malimidwe ndi Zolengedwa akuchita chotheka kuti anthu a dziko lino azipeza phindu lokwanira kuchokera munsomba za m'madzi a dziko la Malaŵi.

M'chaka cha 1978, pafupifupi nsomba zolemera matani 68,000 adazigwira ndipo mwa izi matani 3,306 adazitumiza kumaiko ena.

## FISHERIES IN MALAWI

One third of Malawi is water in lakes, rivers and swamps and Malawi has five lakes--Lakes Malawi, Malombe, Chilwa, Chiuta and Kazuni. There are also many rivers, the most important being the Shire, the only one that flows from Lake Malawi.

The water of the lakes, rivers and swamps yield fish of different varieties for local consumption and export and the catching of fish in Malawi forms an important industry that uses age-old methods and modern techniques yielding tens of thousands of tons of fish.

Fishing provides livelihood to many people in many capacities--actual catching fish, storing, transporting it, trading it and preparing it for consumption. And the English habit of eating "fish and chips" is well established in Malawi.

Fish is a plentiful and relatively cheap source of protein in the diets of many people and there are people who depend wholly on fish for food and livelihood. At the same time, the Fisheries Department of the Ministry of Agriculture and Natural Resources is doing its utmost so that the people of this country can derive the most benefit from the fish of the waters of Malawi.

In 1978, nearly 68,000 metric tons of fish were landed. Of these, some 3,306 metric tons were exported.

Malo wodziwika kwambiri pausodzi wa nsomba molingana ndi mmene amazigwirira ndi ku Nyanja ya Chilwa, m'boma la Zomba. Nyanjayi njosazama konse ndipo madzi ake satuluka kupita kulikonse. Malo ena m'Malawi muno amene usodzi wa nsomba ndi wofunika kwambiri molingana ndi kuchuluka kwake ndi mbali ya kummwera kuvuma kwa nyanja ya Malawi, mbali ya ku Mangochi, mbali ya kummwera chakuzambwe kwa nyanja ya Malawi, ku Nyanja ya Malombe ndi kumtunda kwa Shire, kungsi kwa Mtsinje wa Shire, ku Domira Bay, m'dera la boma la Salima, ku Nyanja ya Chiuta, m'boma la Machinga, ku Likoma ndi ku Chizumulo (zomse ndi zilumba zoyandikana m'nyanja ya Malawi ndi mbali ya boma la Nkhata Bay), ku Karonga ndi ku Chilumba kudzanso m'magombe wozungulira nyanja ya Malawi ku Nkhata Bay.

Pofuna kugwira nsomba, Amalawi ali ndi njira zosiyanasiyana zakale ndi zatsopano zomwe. Koma njira yodziwika kwambiri ndi yogwira ndi matchera amene amagwira nsomba m'makha zikati ziyesere kupyola ukonde.

Makoka ndi amene amazungulira nsomba pamalo m'nyanja nkuzikokera kugombe kumene amakazikhuthula.

Maukonde wokhala ngati thumba amakokolola nsomba mkati mwa nyanja nkumakazikhuthulira m'mabwato.

Ndiye pali mtundu wina wakalekale wodziwika ndi dzina loti chilimira womwe susiyana kwenikweni ndi uja wonga thumba.

Asodzi amene amapha nsomba zambiri za malonda amagwiritsa ntchito ukonde wokhala ngati thumba pomangirira kumabwato awiri amene amayendera pamodzi pantunda wotha kuutsekula kokwanira.

Kungsi kwa mtsinje wa Shire anthu amagwira nsomba m'miyono, m'maukonde woponya ndi ena wokhala ngati thumba molingana ndi nyengo ya chaka.

The most important fishing areas in Malaŵi in terms of tonnage include: Lake Chilwa in Zomba District. This lake is relatively shallow with no outlet. Other important fishing areas of Malaŵi in order of their importance are the South East arm of Lake Malaŵi, that is Mangochi area; South West arm of Lake Malaŵi, Lake Malombe and Upper Shire, Lower Shire River, Domira Bay area in Salima District, Lake Chiuta in Machinga District, Likoma/Chizumulo (which are twin islands in Lake Malaŵi and part of Nkhata Bay District), Karonga/Chilumba on Lake Malaŵi and part of Nkhata Bay area on Lake Malaŵi.

In catching fish, people in Malaŵi use all types of methods including traditional ones but the most important ones are: gill nets (matchera) which catch fish by the gills as they try to pass through the mesh of the net.

Drag nets (khoka) are ones that surround fish on a portion of the lake and draw it towards the beach where it is hauled.

The ring net surrounds fish in the middle of the lake and traps it by closing the bottom of the net forming a shallow basin from which the fish is scooped into boats.

Then, there is the traditional type of sein net--Chilimila--which uses a principle similar to that of ring nets.

The trawl net is the one used by commercial concerns. This is a bag shaped net the mouth of which is tied to two boats sailing side by side at a distance enough to open it.

In the Lower Shire marshes fish traps, Castnets and Scoopnets are used extensively at certain times of the year.

Nsomba ndi zoyenera kuziteteza ngati tifuna kuŋi ana athu a mtsogolo  
nawonso adzakondwere nazo. Boma lidapanga malamulo woteteza nsomba  
(Cap. 66.06) kuwona m'mene anthu akuzigwirira ndi kufufuzanso za madera  
amene nsomba zimapezeka zambiri.

499



Fish is a resource which must be protected to ensure that future generations will enjoy it. Government controls fishing through Regulations under the Fisheries Act (Cap 66.06) and the monitoring of the fish landings from areas where fish stocks are assessed scientifically.

### 3. ADMARC INAGULA MBEWU ZA ALIMI

Alimi wamba a m'midzi m'dziko lonse lino la Malaŵi, pamodzi ndi eni maesiteti ndi mafamu aakulu; amapeza zokolola zambiri, monga chimanga, fodya, mpunga, mtedza, nyemba, thonje, mapira ndi mbewu zina zotero; zomwe zambiri mwa izo amazigulitsa kuti apate ndalama.

Mwaŵi wake ngoti, angakhale kuti mlimi wamba aliyense amakolola michepekedwa; komabe amathandiza dziko lino potumiza zokolola zakezo kumaiko akunja. A Bungwe la ADMARC amatsegula misikaponseponse nku-magula mbewu zonse zimene alimiwo angalime.

Panthaŵi yomweyonso, Mtsogoleri wathu wa dziko lino la Malaŵi Ngwazi Dr. H. Kamuzu Banda wakhala akunena nthawi zonse kuti anthu akefe tilimbikire kulima kuti dziko lino lisangokhala ndi chakudya chokwanira chokha; komanso chakudya china chizitsala kuti tizikagulitsa kumaiko akunja kuti tikhalenso ndi ndalama zochokera kumaiko akunjawo.

Amalaŵi amvera pempho la Ngwazi ndipo padakali pano zokolola zawo zimakhala mbewu zabwino ndithu. Mbewu zofunika kwambiri zimene Amalaŵi amalima ndi monga chimanga, mpunga, nyemba, kabaifa, ndiwo za mtundu wa nyemba, chinangwa, khofi, mkondadzūwa, mapira, mawere, chitowe ndi mbewu zina.

Pofuna kugula mbewuzi kuchokera kwa alimi, Bungwe la ADMARC lili ndi madepoti 12; ndipo ikakwana nthawi yokolola dzinthu; limakhazikitsa misika yokwana 903 kumadera onse m'dziko muno kumene amalima mbewuzo; ndipo yambiri mwa misikayo amatsekula kumadera a kumidzi.

## ADMARC BUYS SMALLHOLDERS' CROPS

Smallholder farmers in the villages throughout Malawi as well as estate and large farm owners every year produce great quantities of maize, tobacco, rice, groundnuts, beans, cotton, millet and other crops most of which are sold for money.

Fortunately for the smallholder farmers whose individual produce is not large but who nevertheless contribute to the exports of this country, the Agricultural Development and Marketing Corporation (ADMARC) provides ready markets for any quantity they may produce.

At the same time, the Malawi leader, Ngwazi Dr. H. Kamuzu Banda, has always emphasized that people should use the land fully so that the country is not only self-sufficient in food but there is surplus for sale abroad to earn foreign exchange.

Malawians have responded to the Ngwazi's appeal and are now producing good quality crops. The main crops Malawians grow are; maize, rice, beans, peas, pulses, cassava, coffee, sunflower, sunsun, sorghum, millet, green gram and sesame seed among others.

To buy all these crops from farmers, ADMARC has 12 main depots and at the height of the harvesting season establishes over 903 markets in the farming areas all over the country most of which are in very remote places.

In bringing the markets close to the farmers, ADMARC enables them to see the demand that their crops command. This in turn encourages smallholder farmers to produce more and good quality crops. Some even aspire to go into commercial farming.

Potsegula misika kufupi ndi alimiwo, Bungwe la ADMARC limawathandiza alimi kuti aone kufunika kwa mbewu zawo. Zoterezi zimawaimbikitsa alimi kuti azilima mbewu zambiri ndi kupezanso mbewu zabwino kumalonda. Alimi ena pamafika pofuna kutsegula mafamu aakulu kuti azipata ndalama zambiri.

Titapita kumisika ya ADMARC timangoona anthu ali thukuta kamukamu, komabe amakhala alimi aakazi ndi aamuna wosekerera; akutenga mbewu zawo kudzagulitsa nkumalandira ndalama. Amasekerera chifukwa amadziwa kuti akhala ndi ndalama m'matumba mwawo zogulira zovala zabwino, kumangitsira nyumba zabwino ndi kutumiza and awo kusukulu; mosaiwalanso kubweza ngongole za boma ndi kugula zipangizo zofunika pantchito ya ulimi pokonzekera zodzabzyalanso mbewu zina mtsogolo.

Amalawi alimbikitsidwa ndi boma kuti awonjeze zakudya monga chimanga; osati powonjezera maekala ambiri ayi; koma potsata malimidwe a makono kuti azigulitsa zakudya zotsalazo nkulimanso mbewu zina zimene zimabweretsa chuma chambiri paekala imodzi.

Mbewu zikachoka ku misika amazitutura ku mashedi ndipo kumeneko amazitumiza kumadera kumene zingafunike kwambiri; kapena kuzitumiza kunja kwa dziko lino. Mashedi amene alipo pakali pano ali ndi malo aakulu okwana makyubiki fiti 25 miliyoni.

Kumisika ya ADMARC ndi kumadepoti ake samangogula mbewu zokha ayi; komanso amawagulitsa alimi zipangizo zofunika pantchito yawo monga mbewu zosankhidwa bwino, feteleza, mankhwala wophera tizilombo, makina wopopera mankhwala, ngolo, mapulawo ndi zipangizo zina. Mwa njira imeneyi, alimi amathandizidwanso chifukwa sawononga ndalama zambiri zofunika paulendo zimene akadagwiritsa ntchito atafuna kukagula zinthuzi kumatawuni.

The scene at ADMARC markets is that of seated but smiling farmers, both men and women, busy bringing their produce for cash sale. They smile because soon they will have money in their pockets with which to buy better clothes, build better houses, and send their children to school, not forgetting loan repayments and the buying of farm inputs in readiness for the next crop season.

Malawians have been encouraged by the Government to increase production of food crops such as maize, not necessarily by increasing acreage but by using modern methods of farming so that they can have a surplus for sale as well as sparing most of the land for cash crops that offer a higher return per acre.

From the markets the crops are transported to storage sheds from where they are distributed to areas of need or prepared for export. The existing sheds have a storage capacity of 25 million cubic feet.

ADMARC markets and depots do not only buy crops, but also sell to farmers farming needs in the form of selected seed, fertilizers, pesticides, spraying equipment, farm carts, ploughs and other farm essentials. In this way, again farmers are saved transport and other costs which they would have incurred were they to look for these in towns.

#### 4. AMAYI PANTCHITO YA CHIPANI NDI YA CHITUKUKO

Chokondweretsa kwambiri ndi choti amayi a dziko lino awonetsa luntha lawo potumikira chipani cha Malaŵi Congress Party ndiponso pachitukuko cha dziko lino.

Tikayang'ana pachiwerengero cha anthu chomwe chidachitika m'zaka za 1966 ndi 1977 tiwona kuti dziko la Malawi lili ndi amayi a zaka zosiyana siyana ambiri poyerekeza ndi amuna. Mwachitsanzo paanthu 5,561,821 amene adawerengedwa m'chaka cha 1977, 2,887,289 adali amayi. Chokondweretsa kwambiri ndi choti amayi amenewa akuthandiza kwambiri pantchito zokweza dziko lino.

Amayi akhala akuthandiza ndi kutumikira molingana ndi miyambo yathu makamaka popeza chakudya angakhale kuti kalero adalibe mphamvu ndi ufindo weniweni pomachita zinthu. Masiku ano, iwo ndiwo amene akutso-gelera pantchito ya ulimi makamaka kumadera a chitukuko.

Kuyambira chaka cha 1958, pamene Prezidenti Wamuyaya, Ngwazi Dr. H. Kamuzu Banda, adakonzanso bwino bungwe lakale la ndale la Nyasaland African Congress, amayi a dziko la Malaŵi akhala akuthandiza kuyendetsa chipani kupyolera m'bungwe la Amayi, lotchedwa Women's League.

Poyambitsa bungwe la Amayi, mtsogoleri wa dziko la Malaŵi adawapatsa mwaŵi wapadera wokhala ndi kufika pomwe ali masiku ano.

## WOMEN'S ROLE IN PARTY AND DEVELOPMENT

One of the most gratifying aspects of independence is the role the women of this country have played and continue to play in the political Party, the Malawi Congress Party, and in the development of the country.

A glance at the census counts of 1966 and 1977 reveals that there are more women in Malawi almost in all age groups. For example out of a population of 5,561,821 in 1977, some 2,887,289 were women. It is pleasing to note that this majority plays more than its full share in the country's affairs.

The women have always played an important role in our traditional society especially in the production of food though in the past they did not have a strong voice in the community. Today they take a leading part in farming, especially in the development project areas.

Since 1958, after the return home of His Excellency the Life President, Ngwazi Dr. H. Kamuzu Banda, who reorganized the old Nyasaland African Congress, the women in Malawi are part and parcel of the political movement through the League of Malawi Women, which is otherwise known as the Women's League.

By forming the Women's League, the Malawi leader gave the women that rare opportunity to be what they are now--"a political and social force," to use the Ngwazi's own words.

Chipani cha Malaŵi Congress Party chomwe chidalowa m'malo mwa chipani chakale cha Nyasaland African Congress chili ndi zigawo zitatu: Bungwe Lalikulu, Bungwe la Amayi ndi la Achinyamata. Chipanichi chidagawidwa monga phiri la ndonyo imodzi pokhala ndi nthambi m'midzi. Palinso makomiti ku Maeliyo, ku Madisitirikiti, ku Malijoni kenaka ku Likulu kwenikweni. Amayi ali ndi wowaimila m'makomiti amenewa mpaka ku Lijoni.

Pachifukwa ichi, pali amayi amene ali Aphungu a Nyumba ya Malamulo ndiponso Nduna Zazing'ono za Boma. Palinso Makhansala a m'maboma, a m'matauni ndiponso a m'mizinda.

Asungwana a dziko lino ali ndi mwaŵi wopita kusukulu mpaka ku Yunivesite. M'dziko la Malaŵi muli sukulu za sekondale za asungwana wokhawokha khumi pamene ena amakalowa nawo kusukulu zophunzira anyamata ndi asungwana.

Asungwana ambiri amatsiriza maphunziro awo ku Yunivesite ya Malawi chaka chilichonse. Chokondweretsana china ndi choti m'chaka cha 1978, asungwana 378 adalandira madigiri, madipuloma ndi masetifiketi kuchokera kumakoleji a yunivesiteyi. Palinso ena amene adakachita maphunziro wosiyanasiyana kumayunivesite a maiko a kutsidya la nyanja.

Amayi akulowa ntchito zosiyanasiyana--ya uphunzitsi, ya banki, ya m'sitolo--poonjezera pa ya Unamwino, yomwe yakhala akuilowa chiyambire kalekale. Masiku ano asungwana akukowanso ntchito ya Upolisi, imene kale sankaganizira konse. Nawonso a Capital City Development Corporation, ku Lilongwe ndi wonyadira kwambiri pokhala ndi mayi woyamba wa Chimalawi yemwe ndi Mlembe wa bungweli m'dziko muno.



The Malaŵi Congress Party which replaced the old Nyasaland African Congress has three components: the main body, Women's League and League of Malaŵi Youth (or Youth League). The Party is organized in the form of a pyramid, with branches at the village level. Then there are area committees, District Committees, Regional Committees and ultimately the National Executive Committee. Women are represented in these committees up to regional level.

As a result of this, women are Members of Parliament as well as Parliamentary Secretaries. They are also District Councillors, Town Councillors and City Councillors.

The girls of this country have opportunity to go to school up to the university. There are ten girls' secondary schools in Malaŵi, while more girls are admitted to co-education secondary schools which take both boys and girls. Many young women graduate from the University of Malaŵi each year. In fact some 378 young women have obtained degrees, diplomas or certificates from constituent colleges of the university up to 1978. There are others who have qualifications from overseas universities.

Women have gone into various professions--teaching, banking, commerce--apart from the traditional profession of nursing. In fact a growing new field is that of the Police Force, a thing that was not thought of for women. The Capital City Development Corporation in Lilongwe prides itself in appointing the first woman Company Secretary in the country.

Amayi nawonso ali kalikiyiki pantchito za bizinesi kotero kuti masiku ano ali ndi sitolo zawozawo, mabizinesi wonyamula anthu ndi akatundu womwe angakhalenso magalaja.

Chinthu chachikulu chomwe Prezidenti Wamuyaya adachita pamene adabwera kuno kwawo ndicho kuyambitsanso kuti anthu azisunga bwino miyambo yawo. Iye adanena mosakuluwika konse kuti tisamachite manyazi ndi magule athu kapena kulola kuti miyambo yathu ipotere monga momwe amishoni ankafunira. Izi amayi adazitsata popanda chovuta chionse kotero kuti sadangotsata miyamboyi kokha ayi, komanso adaikometsa molingana ndi chitukuko cha dziko lathu lino.

Masiku ano amayi amavala zovula za makono akamavina magule a makolo athu ndipo amapeka nyimbo za tanthauzo zofotokoza za moyo wa makono potsatira momwe ankavinira makolo athu--izi amazichita pofuna kusonyeza chitukuko chomwe chachitika ndiponso chomwe chikunkabe mtsogolo.

Kupita mtsogolo kwa amayi a dziko lino la Malaŵi, kwachitika chonchi chifukwa cha Nkhoswe yawo Nambala Wani, Ngwazi imene idaika maziko abwino a chitukukochi.

Poona zomwe amayi akhala akuchita chilandilire cha ufulu wathu, tiwona kuti iwoŵa akuchita zotheka pothandiza pantchito za chitukuko cha dziko lino ndipo ndi chodziŵikiratu kuti iwo adzapitirira kuzichita izi mpaka mtsogolo muno.

Women have also entered business and commerce in a big way, so that they own shops, transport companies and even mechanical workshops.

One of the main things that His Excellency the Life President did when he returned home was to revive our culture and told us not to be ashamed of our traditional dances and values as missionaries wanted us to. Women responded to this very well so that not only has our culture been revived but women have even improved on it in line with the general development of the country.

Women use modern attire when dancing the age old dances of our ancestors. They compose songs in the contexts of the old dances to describe a modern situation--to demonstrate progress and development with a keen eye to the future.

The prospects for advancement for the women of Malaŵi are bright as their Nkhoswe Number One, the Ngwazi, has laid the foundation for their progress.

From what they have done since independence, it is clear the women take the opportunities and move with the country's development. And surely they will continue to be "a force" in all fields of activities.

## B. CHAKUDYA CHABWINO CHOYENERA KUPATSA BANJA

### KUFUNIKA KWAKE KWA CHAKUDYA CHOYENERA

#### Chifukwa chiyari timadya chakudya?


Thupi la munthu monga m'mene zili zomera, limafuna chakudya chokwanira ndi choyenera nthawi zonse. Munthu amene sakudya chakudya chokwanira ndi choyenera amakhala ofooka ndi odwaladwala.

#### Pali chakudya cha mitundu itatu chimene chimafunika m'thupi la munthu:

1. Chokulitsa ndi kulimbitsa thupi.
2. Chopatsa mphamvu.
3. Choteteza thupi kumatenda.

#### Ndi chakudya chiti chimene tiyenera kudya kuti tikhale a mphamvu?

Kuti tikhale a mphamvu, tiyenera kudya chakudya chokulitsa ndi cholimbitsa thupi 'protein'. Kawirikawiri m'chakudya chatu mumakhala mulibe chakudya chokulitsa ndi cholimbitsa thupichi. Chakudya chokulitsa ndi cholimbitsa thupi tingachipeze m'nyama, m'nsomba, m'mazira, mu 'cheese', m'mkaka, m'mbewa, m'inswa (ngumbi), m'mafulufute, m'ziwala, m'nkhululu, m'nyenje ndiponso m'chakudya chomwe cha m'gulu la nyemba ndi mtedza.



## PROVIDING GOOD FOOD FOR THE FAMILY

--FROM 'A GUIDE TO HEALTH AND GOOD  
FOOD FOR THE FAMILY' BY CORNELIA  
VAN SCELVEN FOR EXTENSION AIDS

### THE NEED FOR A BALANCED DIET

#### Why do we eat food?

The human body is a living thing and like a plant it requires not only a regular supply of food, but also a sufficient supply of the right kinds of food. A person who does not get enough food or food of the wrong kind will be weak and sick.

#### What are the three main purposes for which the body requires food?

1. Body building foods or protein: to provide materials for growth and repair.
2. Energy foods or carbohydrates: to provide materials for energy and warmth.
3. Protective foods or vitamins: to provide materials for health and protection.

#### What kinds of food do we need to eat to have strong muscles, healthy skin, good teeth and nails?

We need body building foods - protein. The Malawi diet is often short of protein. Proteins are obtained from two sources:

animal origin - meat, fish, eggs, cheese, insects, milk  
vegetable origin - peas, beans, groundnuts

Chifukwa chiyani amayi apakati, a wana aknanda ndi wana afunika kumadya chakudya chambiri cholimitsa ndi chokulitsa thupi tsiku ndi tsiku?

Amayi apakati ndi a wana aknanda afunika kudya chakudya chambiri chokulitsa ndi cholimitsa thupi kuti apange mwana ndi mkaka wambiri wakuti mwana aziyamwa. Wana afunika kudya chakudyachi chifukwa akukula. Wanthu odwala kapena amene akuchira kumene afunika kudya chakudya cholimitsa thupi kuti apeze mphamvu. Ndi chakudya cha mtundu wanji chimene tingadyere njala kiti tipeze mphamvu ndi kutenthetsa thupi?

Kuti tipeze mphamvu tiyenera kudya chakudya monga chimanga, mpunga, mapira, mkate, 'buledi', chinangwa, mbatata ndi ntochi. Chakudya cha mafuta chimapatsanso mphamvu koma timafuna chapang'ono.

Kodi tiyenera kudya chakudya chopatsa mphamvu chochuluka bwanji?

Munthu amene amagwira ntchito yathukuta kapena kusewera, ayenera kudya chakudya chochuluka chopatsa mphamvu. Koma amene amangokhala akadya chakudya chambiri ndiye kuti amanenepa kwambiri. Tsono, muyeso wa chakudyachi, uyenera kukhala malinga ndi ntchito imene munthu amagwira ndi msinkhu wake.

Chifukwa chiyani chakudya choteteza thupi kumatenda chili chofunika m'thupi la munthu?

Chakudya choteteza thupi ndi chofunika chifukwa chimathandiza thupi kuti lizigwira ntchito yake bwino. Chakudya choteteza thupi kumatenda chimapezeka m'zipatso monga phwetekere, mapapaya, mango, malalanje, maungu ndi kaloti, ndiwo za masamba monga kholowa, khwanya, mtambe, mnkhwani ndo bonongwe. Mchere umene pachigerezi amati 'calcium' ndi 'iron' ndi ofunikanso m'matupi athu.

Why do expectant and nursing mothers and children need extra supplies of body building foods everyday?

Expectant and nursing mothers need extra protein to make the baby's body and the milk to feed the baby. Children need it because they grow fast. People who are sick or recovering from illness need extra protein to give them back the strength they have lost.

What kind of food do we need to eat to satisfy hunger and provide energy and heat?

We need energy foods - carbohydrates - such as maize, rice, millet, cassava, bread and bananas. Such foods are called staple foods. Fats and oil also give us energy but we only need a little of them.

How much do you need of the energy giving foods?

This depends on the kind of work you do, your age and the size of your body. If you do a lot of hard work or play a lot of games, then you need more of these foods. If you are sitting all day but still eat a lot of carbohydrates you will not use up the energy and they may turn to fat on your body.

Why are vitamins important?

Vitamins are important as they help to regulate our body functions for good health. We sometimes call fruit and vegetables 'protective' foods because the vitamins they contain help our bodies to fight disease. Dark green leaves are especially good as are red and yellow fruits and vegetables (i.e., sweet potato and bonogwe leaves, tomatoes, paw paw, orange, pumpkin, carrot, and mango).

As well as proteins, carbohydrates, and vitamins, we need to have small amounts of some minerals in our diet, in particular calcium and iron.

Kodi ndi chifukwa chiyani mchere wa 'calcium' ndi wofunika m'chakudya chathu?

Mchere wa 'calcium' ndi wofunika m'chakudya chathu chifukwa umapanga mafupa, mano ndi zikhadabo. Mchere wa 'calcium' umapezeka munkaka; matamba amene ting dye ndi minga yomwe, mawere, mchewere, chana ndi ndiwo za masamba zobiriwira kwambiri.

Kodi nchifukwa chiyani timafuna mchere wa 'iron' m'thupi mwathu ndipo tingaupeze m'chakudya chiti?

Mchere wa 'iron' ndi ofunika m'magazi chifukwa munthu amene ali ndi mchere ochepa wa 'iron' m'magazi ake, amakhala ofooka. Mwachitsanzo, ngati munthu ataya magazi pangosi, pobereka kapena podwala matenda a chitopa amafooka kwambiri. Ngati mchere wa 'iron' uchepa m'thupi mwathu, timadwala matenda ochepa magazi. Mcherewu umapezeka m'ndiwo za masamba obiriwira, m'chiwindi, muntima, muimpsyo ndi m'mazira.

#### KUKONZA CHAKUDYA

Kodi munthu adye chakudya chochuluka bwanji patsiku?

Chakudya chimene munthu angadye patsiku chiyenera kuchuluka malinga ndi:

1. Zaka ndi msinkhu wake wa munthu.
2. Ntchito imene munthu akugwira.
3. Chakudya chimene munthu akonda ndi chimene sachikonda.
4. Kupezeka kwa chakudyacho.

Amuna amadya kwambiri kuposa akazi. Wana ayenera kudya chakudya chambiri chifukwa akukula. Amayi apakati, a wana akhanda, wana ndi wodwala afunika kudya chakudya choyenera.



Why do we need calcium in our diet?

Calcium is needed for the good formation of bones, teeth and nails. It is found in milk, small fish (if eaten whole with the bones), finger millet, chick peas and dark green leaves.

Why do we need iron and what should we eat to get it?

If we do not get enough iron in our food we get 'anemic'. Iron is needed in our blood and if we lose blood by accident or at the birth of a baby or by suffering from hookworm, we can get very weak. Good sources of iron are dark green vegetables, liver, heart, kidney, and eggs.

### PLANNING MEALS

How much food should be eaten daily?

The amount of food eaten by a person each day will vary and is determined by:

- 1) age and size
- 2) the kind of work the person does
- 3) personal likes and dislikes
- 4) availability

-- Men, because they are bigger, usually need more food than women. Children, because they are growing, need a lot of food. Expectant or nursing mothers, children and sick people have special food requirements.

Everyone in the family should have a 'balanced diet'. What does this mean?

Everyone should eat something from each food group if possible at every meal and at least everyday. This will give the family a balanced diet and their different food requirements will be met. Meals should be planned beforehand, to make sure that a sufficient variety of foodstuffs is available.

Kodi tikati chakudya choyenera titanthauza chiyani?

Aliyense aynera kudia chakudya cha magalu atatu chokwanira tsiku ndi tsiku ngati kungatheke. Potero banja limadya chakudya choyenera chimene chili ndi zonse zofunika m'thupi la munthu. Pokonza chakudya onani kuti chakudya cha mitundu yonse itatu chilipo.

CHAKUDYA CHOSAYENERA NDI TSEMPHO

Kodi anthu amadya chakudya cholimbitsa thupi chokwanira?

M'Malawi anthu ambiri samadya chakudya cholimbitsa thupi chokwanira makamaka amayi apakati ndi a wana akhanda, nthumbidwa, wana opita kusukulu ndi anthu odwala.

Kodi ndi matenda wati amene amayamba chifukwa chodya chakudya chosayenera?

1. Kwashiorkor: Iyi ndi nthenda imodzi yodziwika imene imagwira wana apakati pachaka chimodzi ndi zaka zisanu. Nthendayi imayamba ngati mwana angodya chakudya chopatsa mphamvu chokha monga nsima pamene wasiya kuyamwa. Mwana otere sikero yake imatsika ndipo kenaka nkhope, miyendo ndi manja zimatupa ndiponso sakonda kudia.
2. Marasmus: Wana amadwala nthendayi chifukwa choti sakudya chakudya chokwanira. Mwana otere sikero yake imatsika, nkhope yake imaoneka ngati ya nkhalamba maso ake amakhala otong'oka. Tsitsi lake limasosoka, limakhala lofira ndiponso lonyozoloka, amaonda kwambiri komanso amafuna kudia kwambiri.

Suggestions:

1. Show pictures or samples of the different food groups.
2. Plan balanced meals for the family for a week.

POOR DIETS AND MALNUTRITION

Do people eat enough protein?

In Malawi, many people do not eat enough protein, especially expectant and nursing mothers, toddlers, school-going children and sick people.

What diseases are caused by poor feeding?

1. Kwashiorkor: One common form of malnutrition occurs among children from 1-5 years. This disease is caused by a diet which consists mainly of starchy food and contains very little protein especially when there is little or no breast milk. A child suffering from kwashiorkor is underweight and in the later stages the face and limbs are swollen, and the child has little appetite.
